SOME FOLK-LORE
STORIES AND SONGS

IN CHINYANJA

WITH ENGLISH TRANSLATION AND NOTES

BY

R. SUTHERLAND RATTRAY

MEMBER OF THE AFRICAN LAKES CORPORATION, LTD.,
BRITISH CENTRAL AFRICA

WITH PREFACE BY

THE REV. ALEXANDER HETHERWICK, D.D.

NEGRO UNIVERSITIES PRESS
NEW YORK

Originally published in 1907
by the Society For Promoting Christian Knowledge, London

Reprinted 1969 by
Negro Universities Press
A Division of Greenwood Publishing Corp.
New York

SBN 8371-1534-5

PRINTED IN UNITED STATES OF AMERICA

PREFACE BY THE REV. ALEXANDER HETHERWICK, D.D.

THE author of the following book has been for some years located among the Nyanja-speaking tribes of British Central Africa at Blantyre, and afterwards in Central Angoniland. His occupation as a member of the African Lakes Corporation has brought him into close contact with the native population of these districts. He has taken advantage of his opportunities to familiarize himself with the native language, of which he has acquired a very competent knowledge. In the course of his studies he made a collection of native folk-lore and stories which illustrate in the fullest degree the various constructions, idioms and grammatical forms of the language. These he has now published with the coöperation of the Directors of the Corporation.

The book is of value as containing examples of native life, habits and customs which are rapidly disappearing from the country before the advance of civilization and the work of Christian missions. The coming generation of natives will grow up under new influences, and the habits of thought and belief that ruled the lives of their fathers will soon be forgotten. Collections of folk-lore such as this book contains are therefore invaluable for the light they throw on a state of native life that is rapidly passing away.

To get into the heart of the native mind is a task well-nigh impossible for a European. The nearest

approach is made through the media of such collections as the author of the following pages has made. For this reason the book is commended to all who are interested in the study of native African life and habits.

It is further to be commended for its illustrations of the Nyanja language in which the stories, etc., are written. This language is spoken over the greater part of British Central Africa, or Nyasaland Protectorate, and forms the chief means of communication between the natives of the various districts themselves, as well as between the European settlers and the native population around them. It seems likely to become also the *lingua franca* of the whole of the British possessions in Central Africa that border on the Nyasaland Protectorate. The student of this language will find no better way into the heart of the subject he is dealing with than through the medium of these native stories. To facilitate this use of them, a literal translation is added, and notes are appended illustrating and explaining such idiomatic constructions as would be likely to present difficulty to a learner.

The writer of this preface has no doubt but that the book will prove its usefulness to the student of the Nyanja tongue, as well as its interest to the student of native African life and thought.

ALEXANDER HETHERWICK.

BLANTYRE MISSION,
BRITISH CENTRAL AFRICA,
January 1, 1906.

PREFACE BY THE AUTHOR

In the study of this language, the student is fortunate in having two such scholarly works of reference as *A Practical Manual of the Nyanja Language*, by the Rev. A. Hetherwick, M.A., D.D., F.R.G.S., and *A Cyclopædic Dictionary of the Mang'anja Language*, by the Rev. D. C. Scott, M.A., D.D., F.R.S.G.S.; on the other hand, there is a striking want of any good prose work in that language. Of translations of the Bible, and other religious books, there are many, but all such works, in the translation, follow the English text almost literally, and contain so many words from foreign sources as to be of little use to the student who, having mastered the grammar and syntax of the language, seeks to enlarge his vocabulary and knowledge of idiomatic expression by reading some prose work. (The ideal translation of the Bible, or other religious work, would be one in which the English sentence is taken, the meaning got at, and this remodelled and transformed according to the native way of thought and expression.) It is to supply such a want that this little work is intended. The aim throughout has been, in the Chinyanja part, to write each sentence as a raw native would speak it. It is a commonly heard saying, that only boys trained at a Mission talk the language "grammatically." This is correct, if by "grammar" we mean a principle of set rules for the speaking of a language. For to the uncivilized native any such rules as those governing our own, and other languages of civilized countries,

are unknown, and he talks, "having regard rather to the poetical feeling than to the grammatical position and syntax of a word." But enclitics, tense particles, concords, the various forms of the verb (applied, causative, intensive, reversive, etc.), and all those auxiliary particles such as *ba*, *ka*, *ngo*, *dzi*, and enclitic particles such as *-nso*, *-be*, *-tu*, etc., by which all the finer shades of meaning are expressed, he uses absolutely correctly, and it is with a view of understanding, and making oneself understood, to the raw, uneducated element among these natives, that one should go to the trouble of learning this language.

The customs, stories, etc., recorded herein are those of the natives inhabiting Central Angoniland. They are descendants, for the most part through intermarriage with the Achewa, of the Zulus who came from south of the Zambezi, scattering as they advanced, under different leaderships; those under *Gwaza* (the father of *Sakambewa*), and his *nduna Chiwere*, settling at Dowa; *Mpezeni*, a son of *Gwaza*, settling near Fort Jameson. *Mputa*, the father of *Chikusi*, after reaching as far as Lake Chirwa, and raiding the Anguru under *Sinjaubwereka*, came to Domwe, near Dedza, under promise of cattle from *Sosola*, a *Chipeta*, or *Nchewa* chief. (*Chipeta* and *Nchewa* are synonymous, the former word being a sobriquet bestowed on the *Achewa* who came on to the Angoniland plateau, by the *Achewa* who settled on the Lake shore, the latter referring to the former as the *a chipeta*, i. e. they of the *chipeta* (long grass)). Intermingled with these customs, borrowed for the most part by the conquerors from the conquered, are to be found traces here and there, and here and there a word, which strike the key-note of their past history, now all but forgotten even by themselves. But what is of their

past, and what of their present, will be clear to one who has made a more minute study of their Zulu ancestors than the writer had time or opportunity to do. Whatever be of merit in this little work, the writer owes to the Rev. Alexander Hetherwick, D.D., to whose kindness and courtesy in teaching him Chinyanja, when he first came to the country, he owes all that is best in his knowledge of the language.

MANDALA,
BRITISH CENTRAL AFRICA,
January 1, 1906.

CONTENTS

PART I (IN CHINYANJA)

PART II (A LITERAL ENGLISH TRANSLATION)

Part III

PART I

CHINYANJA

(*Note.*—Dialectic peculiarities have been removed or explained.)

I

ZA MWABVI

I. Mkazi wa mfumu akafa [1], kapena atafa [2] mwana wache, apangana [3] kuti, " Inu pam'dzi pano tifuna kuti tiombeze " [4]. Pa mwabvi [5] wa mfumu aitana makosana [6] onse, koma pa mwabvi wa antu achabe amwa antu onse. Akaona palikufa antu, apangana ndi akulu kuti, " Taonani, pa mudzi pano antu alikufa tifuna [7] kuti tikaitane sing'anga adzatilondere [8] pam'dzi pano." Ndipo atuma mnyamata mmodzi kukaitana [9] sing'anga. Abwera madzulodzulo [10]. Amkazika m'nyumba yina, antu osadziwa [11] kuti kwabwera sing'anga. M'mawa, adzukira mnyamata mmodzi, nakaima [12] pa bwalo, atakwera pa chulu, kuti antu onse amve, ndipo ati, " E muyevena [13], musadia nsima lero, yemwe ali m'tulo adzuke [14], adzimva yeka [15], alikuti musambe nonse [16], mulawa [17] kamoa kowawa lero."

II. Yemwe amati achite [18] kadzutsa [19] angotsentseneza [20] ufa wache m'tala [21], ayamba kubisa katundu kuti, " Nanga tidziwa bwanje lero, kumeneko kuti tikabwera " [22]. Ndi mikanda yonse bvule, bvule [23], bvule. Akaona kuti dzuwa lirikuyamba kuturuka, asonkana antu onse. Ndipo ayamba kusankula amnyamata olimba, kuti, " Uje atsale [24], ndi uje atsale, adziyang'anira [25] anzao, ndi kulonda [26] pa mudzi, kuti ana a sing'anga angadzayambe [27] kufumula za antu osafa " [28]. Ndipo ayamba kunyamuka kunka [29] ku ñthañdó [30], nasenzeratu [31] mtondo

ndi munsi wache, (mtondo uli wonse [32]) njira imodzi, pingīni, pingīni [33], nafika pali sing'anga [34], iye nayamba kwandandalitsa; safulatira [35] dzuwa, akazi andandalika mpambo [36] wao, amuna mpambo wao, bi! Sing'anga abvalira [37] myoni [38] yache, ndi machoa [39] a mbuzi, abvalira m'manja. Ndipo anyamuka mkulu ndi chipondamtengo [40], kapena mbuzi, chakumasula tumba.

III. Ndipo sing'anga ati, "Patseni chiwanda" [41]. Ndipo mkulu uja, anyamuka kunka [42] kwa mfumu wa pa mudzi kuti, "Alikufuna chiwanda." Ndipo mfumu uja ati, "Nanga iwe sulikudziwa antu omwe adafa pano." Ndipo mkulu ampatsa kuti, "Pano adafa uje ndi uje, ameneo ndiwo taniitanira" [43]. Ndipo mapondera [44] ati, "Ndipatseni mfiti [45] zimene zidadia ameneo." Ndipo aitana antu awiri [46], mkazi ni mpongo, kuti, "Anapiri, ndi uje, bwerani pano" [47]. Amene aitana'o abwera pafupi pa mtondo. Ndipo mapondera amasula tumba lache la nyani, nasolola kungwa la mwabvi, nabentulira mu mtondo ndi dzino la mvu. Pamene alikubentula, sata kungwa lonse, abentula, nasia. Akabentula, mwabvi ulumpa, ugwa ku dzanja la chikazi, akabentula, ugwa kudzanja la chimpongo [48]. Angodziwa kuti pano lero pali maere, kwa akazi kufa antu, ku mpongo kufa antu. Ndipo sing'anga ati, "Tipatseni antu, akatitungire [49] madzi." Ndipo mkulu uja ati, "Kodi titenge [50] angati?" Ndipo kapena mapondera ati, "Tengani antu atatu, chifukwa antu achuruka." Ndipo auza kuti, "Musakayang'ana mbuyo, mukangotunga, mubwera." (Angazumule [51] mfiti'zo). Pamene wata [52] kutsotsolera m'mtondo, auza mnyamata kuti, "Yamba kusinja." Sasinja ngati [53] mpale, asinja gu', gu', natembenuza munsi. Pamene mnyamata alikusinja, mapondera amagoda [54] mtondo go! go! ndi ndoda yache ya nyani [55], yomwe akumbira dzipatso, nati—

IV. "Kwee, wamvetsa macheana [56],
Macheana Akundamva.
Gwiragwira n'gwankondo [57],
Chidapa nyani ku Bongwe,
Musapera chobvundikira koma chogadamika.
Tumba langa mvetsa mzinje [58].
Wadza [59] m'mudzi ndiwe [60] nkoswe.
Alikuti pano padafa uje ndi uje,
Ameneo ndiwo akwiitanira [61] iwe.
Ali apa, Anapiri, ndi bambo [62] wa kwa uje,
Anapiri, ndiwo [63] atenga denga.
Bambo natenga mpeni,
Kuti musali inu [64],
Pompano. pompano, musanze kuwiri kuwiri.
Kuti muli inu [65],
Tema, tema, tema."

Pamene afika nao madzi'o, atenga mtsuko umodzi nakutulira m'mtondo, tobvu limvekere [66] tu, tu, tu, natenga chiko natunga chiko chimodzi cha mwabvi, namanka alikutakasa [67] ni ndodo yache ya nyani, alikunenera [68] kuti—

"Tola, tola, tola, tola,
Muona loka [69] lakum'mawa, lakumadzulo musaliwona'i [70],
Kodi si ndi'nu uja?
Mudanka ku Dzomba [71],
Mudaimba ng'oma,
Yamvekera ku Mperewera [72] kwa nchenche,
Nchenche ya chilimba.
Kuli buluzi wa ng'ala.
Kuti musali inu, mudamba ng'oma'yo,
Musanze.
Kuti muli inu,
Mufe.

V. "Mudanka kumwamba,
Mudatenga ntsitsi wa dzuwa [73]
Mwayesa [74] mkuzi,
Kuti, 'Ukale chilimbiriro,
Choti ine mwabvi ukadza,
Udzandipambane,
Ndidzakula ine,
Zimenezo, udzidule, dule, dule,
Mudameza dzira la mpungu,
Kuti mwabvi ukadza,
Udzasanduke mterera [75],
Limeneli kaliswe [76].

"Mudatenga ndulu wa ng'ona,
Mwaika mu mtima,
Mudatenga tumba la nsatu,
Mwameza, kuti mupambane,
Iwe kazing'ambe.

"Mudatenga pula,
Mudamata ku pazi,
Kunka m'munda mwa mzanu,
Kukatenga dzintu,
Mulinkunka, nyang'a, nyang'a,
Kukasansira m'munda m'wanu,
Kwa mzanu kuli perete, perete,
Kwanu kuli ti, ti, ti.

VI. "Mukaona mwana wa mzako, akaenda,
Muti, 'Waenderanje,
Koma ndidakamudia' [77],
Ameneo alowe umu.

"Zibade za ku nsitu, mudamenyetsa pamodzi
kuti zisanduke nzulule,
Kodi si ndi'nu aja, mwaimba nyimbo, m'mati,
'Çhikakula, chikakula, chikakula,

Achita kugudubuza,
Kakachepa [78] angonyamula
Si ndi'nu m'matêro?
Kani ine ndimanimva.'
Kalumo kaja mwatenga?
'Yai ndaiwala.

" Chinamwali, chinamwali, e! e! e!
Mudatenga dzikongono dza ana a antu,
M'mamuka, mubvina nazo,
Mbuluzi wa ng'ala ali pa mpando,
Naimba ng'oma,
Kumodzi, kumodzi,
Wazungulira kuwiri [79], wang'amba ng'oma.

" Chienda ndi usiku [80],
Chidadza msana,
Chidamwona."

VII. " Ai taonana lero malire m'pompa [81], la uko n'danga [82], la uko ndilo lanu." Agwada pomwe pali mfiti, sayankula ndi mfiti iyo iyo [83], ayankula ndi a chabe, yemwe walingana naye, nati, " Mwanawe, kodi udautengera kuti ufiti'o, kodi iwe udatenga kuti ulemerere, kuti udzipambana iwe weka?" Pamene alikunyamuka ati, " Ndakugwira, usapulumuka'i, upite muno, upite muno, ulowe umo." Akaona kuti adata kusinja mwabvi, atenga madzi, nakutulira mu mtondo nayamba kutakasa, alikuchotsa masese [84] ache natenga ziko ziwiri, natunga mwabvi. Anapiri aja ndi bambo wa kwa uje, ameneo ndiwo ayamba kumwa. Ndipo amwetsa anzao onse, amuna awiri abwere nadzamwa [85], natunganso, napatsa akazi awiri. Adzamwa chokachokacho [86] mpaka kuta.

VIII. Ndipo mapondera ati, " Kamoa kameneko ndachita kogula, musataya, iai inu, tangonena kuti mulawe, ndi kamtsuko." Ndipo agwetsa mtondo

ndi pazi naimba ndiu [87]. Akaona mfiti imodzi yafa, ati wagwetsa mtondo. Mfiti yina pofa, ingoti, " Uwi, Uwi "; antu adziwa kuti ameneyu adasanduka fisi; akalira ngati mkango, adziwa kuti chinali chirombo chachikulu. Ena pamene alikufa afumbata m'manja. Akafumbata dzanja limodzi, ndipo adziwa ameneyu adadia antu asanu; akafumbata m'manja awiri, adziwa kuti adadia antu kumi. Pamene asanzasanza ata, alumpitsa njira. Akaona walumpa, adziwa ndi muntu, chifukwa anatenga siswiri natsukira mwabvi wache. Ndipo sing'anga ati, " Ngādzimuka [88] ku mudzi tsopano, kwagwa mtengo sikuzimirai " [89]. Yemwe analimbitsa, akaona chimbudzi, nafa. Sing'anga akamva kuti kwafa muntu, amuka konko kukabvula nsaru yache ndi kudula mikuzi. Amene atsala pa nthando, akakala mfulu, ndipo atenga dipo kukaninka sing'anga kuti, " Ndikakwirire." Akakala kapolo ndipo adzatenta. Antu amene adatsala ku mudzi adzamwanso mawa. Mapondera, pamene alinkunka kwao, ampatsa mbuzi, kapena muntu, bambo wache yemwe [90] adafa ni mwabvi. Nsaru zimene akabvula kwa mfiti'zo, anka nazo, atsukira mwabvi wache kuti udzipabe antu. Muntu akafa ni mwabvi satenga mzimu [91] wache ku mudzi, aupitikitsa ku chire.

II

ZA MALIRO

I. Muntu akafa [1], auza antu onse kuti muntu uja watsinzika [2]. Ndipo akulu a pa mudzi asonkana

kunka [3] m'nyumba'mo. Nayamba kusambitsa [4] mtembo, namdzoza mafuta, namuta.[5] Ndipo afuna mwala wa tantwe, naika pa koma, namkazika tsonga pa mwala'po. Ndipo antu ayamba kulira akazi oka ali m'nyumba muli chitanda [6], amuna akala panja, ana m'konde. Alikulira kuti, " Mai wa wa we, mwiyeni wami [7], ndichita [8] bwanje ine lero, mai, mwiyeni wami." M'mawa, pamene kwacha, antu ena atenga makasu ni nsembe [9], anka pa pumulo [10], nafutira nsembe pa tsinde pa mtengo napita, poti pano [11] alikufika pa manda, atola mwala, amene watola'yo, naponya, nati, " Tapita " [12]. Ndipo ayamba kulambula natenga nsembe nalemba litinda [13]. Akata kulemba, nabwera mkulu mmodzi, natema dote, atemanso la kwina, antu ndipo ayamba kukumba. Antu a pa maliro saopana; akafuna kutukwana, angotukwana. Akata kukumba dzenje, muntu akalowa, osaoneka. Pamene akumba [14] dzenje lalitari, aopa mfiti, kuti zingadzamnyamulire [15] pafupi. Ndipo atenga tsekera, lomwe anamyesa nalo, nayesa mudzi [16]. Afula malo ache. Akata abwera akulu kudzasuzumira [17]. Awiri amene akala m'manda'mo, ndiwo [18] adzikulu [19] akulu, amene adzidzagawira [20] anzao zintu zonse.

II. Amene akatenga [21] mtembo amuka alikulira. Ndipo antu amene atsala ku mudzi asonkana, nafika, nalowa m'nyumba'mo, nanyamula [22] mtembo. Ayala mpasa pa komo, namkazika pompo, nanyamulanso, nanka [23] alikumtandalitsa nyumba zimene akakala [24], nanka naye pa bwalo pache, namkazika. Ponyamula apo, n'kupita [25] naye ku manda. Pamene afika pa pamulo, namkazikanso pansi, ponyamula'po ndiye kukafika ku manda. Ponka ku manda, ndipo atsogola amene asenza katundu ndi mpasa. Amene anyamula mtembo amuka alikulandirana. Akafika pa manda apatsira adzukulu omwe adakala m'manda'mo. Ndipo ayamba kubvula nsaru yache,

natenga mwala wa tantwe, namkazikira, natenga mwala wa mpero, namwiika pa mutu. Kuti ali ndi ana [26], āgwiritsa [27] mkala nakaponya [28] m'manda'-mo (chimenechi n'chidetsa-mtima) [29]. Ndipo mkulu atenga kasu, natema mbali yina ndi yina, ndipo antu ambiri ayamba kukwirira, adzukulu alikupo-ndaponda.

III. Akata kukwirira, agulula makasu, nanka ku madzi. Atsogola amene asenza makasu ndi katundu wache wa muntu amene wafa'yo. Pamene afika kumadzi, ayamba kusamba ndi [30] adzukulu, ndipo antu onse, amuna asambira ku mtunda, akazi ku madzi [31], satsulukutana [32]. Pamene ata kusamba, atenga nsaru, ndi njobwe, ndi nsengwa zache zomwe akadiera [33], natenta, fulusa lache nakapiza madzi. Ndipo anka ku mudzi alikulira. Pamene afika ku-manda sing'anga afuna mankwala [34] wakuchotsa chiwanda; natswanya naika m'pale, natsira madzi, napukusa [35]. Mzukulu ndiye ayamba kupaka pa msongolo, ndi m'maso, ndi m'manja, ndimo abwera ena napakanso. Kuti anali ndi ana ache, napaka. Agonanso pa masiye pompo. M'mawa mwache ku-tacha, mwini wache amene wafedwa'yo [36] atenga mbuzi ndi nkuku nakapatsa adzukulu, ndipo ayamba kwayereka [37] antu ndipo ametana mpala. Asolo-kazi [38] anka ku chitangamire [39] kukaruka zitambo zofiira [40], ndi kumeta apo. Antu onse akata kumeta pe, apula nyama, nayamba kupakula. Agonanso pa masiye pompo. M'mawa mwache nayamba kuola fulusa, adzukulu oka ndiwo aola, nakataya ku mpa-mbano. Ndipo antu abalalika.

IV. Asolokazi akala pa masiye; adzukira m'ma-wa ndi madzulo kukalira kutengo; akakomana ndi antu afuka nsaru ku mutu. Adzukulu ndi akulu a pa mudzi ndiwo alekana malo ndi akazi ao. Aka-kala, kapena mwezi umodzi, akulu apangana kuti anyike [41] chimera. Asanayambe [42] kupika moa akulu

anka ku ula[43] kukaombeza[44], kuti, Tirikutereka moa pa moto, kaya udzapsya bwino, osachita ntenya[45], ndi antunso asadzayamba ndeu." Ndipo wa ula alandula[46], kuti, "Moa udzapsya bwino." Ndipo afunsanso pompo kuti, "Mkazi amene adzatereka moa pa moto nd'ani." Ndipo wa ula aombeza, nati, "Koma, Anapete[47] ndiwo akatereka moa." M'mawa natereka moa, m'mawa mwache napikitsa, lachitatu nuswera[48], la chinai nabviira. (Moa wa chabe, ukakana kuwira, asweretsanso, koma moa wa maliro, ungakane kuwira angopikabe[49].) Tsiku limenelo ndilo amema[50] masewera, nauziratu[51] antu onse kuti moa wapsya madzulo ache. Ndipo asonkana antu onse nayamba kubvina chamba. Apempa "chikoleza moto," ndi "kutsira ng'oma." Akabvinabvina[52] pabwera[53] mkulu nati, "E! machete!machete! mwasonkana antu onse pano, taonani ife ndife antu olira, pasaoneka wina amene achita ndeu; yemwe ali ndi chigololo, akachitire[54] kwao." Pamene kwacha ndiye kuturutsa chisamba m'maso[55]. Pamene dzuwa lifunda asonkana adzukulu onse ndiye kuturutsa nkali imodzi ya moa imeneyo ndiyo chanjero[56], natenga natira m'pale amasandutsa madzi, kuti adziyerekera[57], akayereka nakameta bwino anzache. Akazi alikumeta ku nyumba ya masiye. Asolokazi oka ndiwo akameta ku tengo ndi kubvula[58] zitambo zofiira, nabvala zina za mafuta, napita kumadzi kukasamba. Ukakala moa ulipo, achezeranso, kuti ute msanga, antu alowe m'zimpasa. Asolokazi sapitanso kutengo kukalira, yemwe afuna chigololo angochita, koma pamene alikuchita abvula zitambo za mafuta.

V. Akagonanso mwezi umodzi ndipo ayamba kufulamiza akazi kuti, "Tsopano kangazani chimera." Moa umeneo ndiwo "wobweza mzimu"[59] ndi "wogwetsera nyumba." Ukapsya, akazika m'nyumba ya tsopano, yomwe adamangira pa mbali ya

nyumba ya siwa (siwa = masiye). Akulu nasonkana m'nyumba'mo nati, "Nyumba yanu nai[60], mudziyang'anira[61] ana'wa, osamati[62] akaenda, mukamgwetsa[63] ku chipanda; mukafuna kupempa kantu, mutumiza njoka mshawa, kapena buluzi kapena tonkwetonkwe (nadzikambe), ataona[64] chimenechi, ndiye kukaombeza ula, wa ula ati ndi mzimu wa mbale wache, ulikupempa moa." Pamene amwa ata moa ndiye kuonga kuti, "Yewo pete[65], yewo pete." Adzukulu ndiye kuyamba kugwetsa nyumba ya masiye, akagwetsa natenga madzi nasamba m'manja. Ndipo atenga kankali nakumbira pa komo pa nyumba ya masiye, naika nkali pomwepo, nakwirira, ingooneka miromo yoka, nabōla, ndiye kutenga moa, natira m'nkali'mo, upitirira pansi, natenga pale, nabvundikira, natenganso chitseko, naika pompo, natenga nsungwi, azika pa chitseko, natenga chiko, achola mtibo wache, nakoloweka ku nsungwi. Akata dzimenezo naturutsa moa wa adzukulu, nabvina chamba, kapena cha chitoto[66].

VI. Tsiku limeneli ndilo asolokazi aonana ndi antu a amuna. Chaka china alima oka, ndipo paturuka mkulu wina kudzauza[67] kuti, "Maliro m'bakale[68], tsopano chitani chimera, ndi kugana[69], madzi akatayika saola." Ndipo ayamba kufulamiza moa, ukapsya nabwera adzukulu onse, alikuchezera chamba. Asolokazi alawira mamawa, natenga mtsuko wa moa, anka nao ku madzi nabvula zitambo, atenta, nazimitsa ndi moa. Ndipo akulu asonkana nati, "Tiyeni titenge chokolo[70] tsopano." Nauza mchembere zazikulu zikulu, kuti zipite kuka[71], zikauze akazi kuti auje alikufuna kulowa m'chokolo. Akazi poyamba, nakana, kuti "I'e sitifuna'i tidakalira"[72], ndipo mchembere zipita kukanena ku bwalo. Amuna nati, "Kodi atero," natenga ndodo zao napatsa mchembere. Mchembere zipitanso kwa akazi, naturutsa ndodo. Ali[73], "Iyi nja uje[74], iyi

nja uje." Nasankula imodzi ya mwanna yemwe alikufuna. Akalandira, mchembere zituruka kukanena kuti, "Chokolo chalira uje." Iye mwanna'yo atumiza antu kukaturutsa moa ku nyumba ya akazi. Mwanna yemwe wamkonda napita ku sing'anga, kukapempa mankwala, natenga chipondamtengo [75]. Sing'anga nampatsa kuti, "Koma ukayambe kusambitsa mkazako wa kale, usanalowe m'nyumba ya mkazi wa masiye." Natenga mankwala nakapatsa akazache akale nati, "Nao mankwala [76] udzisamba" [77]. Iye napita ku nyumba ya mkazi wache wa tsopano, natenga pale, natereka pa komo. Likafunda, natira madzi, atenga mankwala, atira momo, nayamba mwanna kutsopa, napaka mwendo. Mkazi nachita chokachokacho [78]. Mankwala ena ali m'mbia, mkazi napukusa, nanyamula, nanka nao ku mpambano, nayamba kusamba mwanna, akata, nabweranso mkazi nasambanso. Madzulo, atenga nkuku yeikazi, naponya ku myendo [79] nagonana. M'mawa mbale wache wa muntu amene adafa'yo adzatenga nkuku, kunka nayo ku nyumba ya mai wache. Mzimu utsatira [80] nkuku'yo. Mwanna akakalakala, akafeza mkazi 'yo ngoipa angolekana naye, anzache angoti, "Wangotenga mauta oka." Mkazi akafuna kukwatiwa [81], ni mwanna wina, angokwatiwa naye osachitanso [82] mankwala.

III

ZA MALIRO A MFUMU A NGONI

I. Mfumu ya dziko lonse ikafa [1], sauza antu a pa mudzi msanga, atsogola atumiza [2] mitenga m'midzi yina kukauza [3] antu, kuti "Tambo lagwa lero" [4]. Pamene atero [5] aopetsa kuti [6] "Tikauza msanga amnyamata'wa, anganke ndi kuchita [7] chiponde cha mfumu" [8]. Ndipo antu onse asonkana mabwalo mabwalo [9], zikopa ziri m'manja, abvalirabvalira [10] ndi myoni [11] yao, ndi dzipandya [12] dza mbuzi, kuli mbu, ngati [13] abvalira dama, kwina [14] ali maliro. Ndipo akulu amkumatitsa [15] mfumu, namgwiritsa m'masaya, natenga chiko chaching'ono, namgwiritsa m'dzanja. Pakumsambitsa atenga udzu wa pa dambo. Sasambitsa tupi lonse, angombulula [16] ku maso koka. Satunga madzi a pa chitsime, omwe amwa antu, akatenga [17] madzi a mu'mfleni [18], oenda [19]. Samdzoza mafuta m'tupi lache. Ndipo atenga nyongo, nambveka, m'mutu monse mbu, natenga chikopa cha ng'ombe, yakupa lero lomwe, namuta [20] nacho. Samfunditsa ndi ku mutu komwe [21], angolekeza m'kosi, natenga mseso [22] wa ng'ombe, nambveka. Ndipo amkazika pa mwala, natenga moa natira m'chiko chija.

II. Mtembo ukala m'nyumba masiku anai, masiku ameneo nkondo irikuguba [23], osaleka'i. Mtembo ukayamba kununka, atenga mafuta namatsira [24] m'mbale, natenta. Tsiku la chisanu ndipo anyamula mtembo, mwana yemwe mfumu [25] adati "Uyu ndiye adzakala mfumu," amene'yu ndiye atsogolera, abale ache onse amtsata pambuyo ndi akazi a mfumu wakufa'yo. Nkondo irikudza, irikusupa [26] mabwalo mabwalo [27]. Anyamula mtembo, ndi akulu akulu,

amnyamula chatsonga. Akafika naye [28] pa madzi po, mfleni ukakala woenda, satseka, ukakala waung'ono, atseka ndi miyala ndi dhote, ndipo kumzi kuuma gwa. Ndipo ayamba kuyala nkuni pa tantwe, natenga mtembo nagoneka pamwamba, natenga nkuni zina nachinjikiza nazo ku mpepete. Pamene ata kukundika nkuni, mkulu mmodzi wa imvi apeka moto [29], ukagwa, akoleza, nayatsa, moto umveke tolo! tolo! Mwana uja amkazika komwe kuli kulowa utsi kuti umtsire. Aima ni mwendo umodzi, chikopa chache agwira m'manja. Moto, ukapulika antu ati, "Zi!" Alikuguba alikuimba nyimbo zao alikuti—

III. "Ndawa iseye,
Waziva zitini mkazi wa ndota [30],
Yeswa."

"Chayani [31] mikondo kwa Afo [32],
Hayo, hayo, ho.
Chayani mikondo kwa Afo,
Wamsia,
Wamsia, m'pakati."

"Wamperekeza Humba'yo [33],
Wadia nyanga Humba'yo."

Chikopa chache chomwe akagwira [34] atentera pambali pamodzi ndi misewenzi. Moto ukanyeka, ndi mtembo omwe ukapserera ndi kusanduka [35] makala oka oka, akapiza madzi. Kuti anatseka [36] mfleni, agamulira madzi, fulusa lonse lipita pa kumsi pa *Mawi* [37]. Akaona kuti ata, apa nkosa natenga chipande nachinjizira [38] magazi, nakazika pompo. Nasenda nkosa 'yo, natumbula natenga chipfu nakutulira pa mwala pompo nayamba kuzira. Nyama adia akulu akulu oka. Akata ndiye kuchoka, kunka ku mudzi [39], napa ng'ombe zambiri, antu adakagubabe [40]. Achotsa zimbudzi nyumba żónse za masiye.

IV. M'mawa mwache nameta makosana [41] onse, ndipo antu a m'midzi ameta. Asolokazi [42] abvala zitambo zofiira. Ndipo aswera [43] masiku atatu, la chinai ndiye kusonkana antu onse mfumu wa tsopano naima pa bwalo pa mwendo umodzi. Ndipo mkulu mmodzi anyamuka nati, "E, muyevena [44], inkosi yanu ya tsopano ndi Pete" [45]. Ndipo antu onse ati "Baiete." Zikopa zao zimvekere [46] li, li li, kuli biriwiri. Akulu akulu natenga mwana kunka naye ku nyumba, kukamlanga kuti, "Lero watsala weka, usunge antu ako bwino, ngati chomwe adachita nao bambo wako. Muntu akalakwa, umamkululukira, koma kulakwa kuchita chigololo chimenecho ndicho choipa, chosakululukika" [47].

IV

ZA UNAMWALI

I. Butu akakula, akakala [1] pa njira. Muntu amene apita pompo, ampeza, ali kale [2]. Akakala mwanna, akauza [3] mkazi kuti, "Ndatola nyama yanga, iri apa, takanyamulani." Mchembere imuka kukalankula naye, ampeza nsaru yache iri gudu! gudu! osapendulizai [4]. Ndipo mchembere 'yo idziwa kuti ameneu wakula, namtenga kunka naye ku madzi [5] kukamsambitsa [6]. Pobwera naye [7] ku [8] madzi'ko, amwiika m'nyumba mwa mbuya [9]. (Amene wamtola'yo ndiye pungu lache). Ndipo anka, nakauza mchembere zina kuti "Mwana uja wakula." M'nyumba'mo agona masiku asanu ndi limodzi. Namwali'yo, akakala wa kwa Kwooni [10], ampatsa nsi-

ma ya mapira oka, akakala wa mfunda [11] wa chabe, ampatsa nsima iri yonse [12]. M'ndiwo zache satira mchere [13]. Nsima adiera [14] m'chipapa ndiwo m'pale. (Chipapa chomwe adieracho adzataya tsiku loturuka m'tsimba [15]).

II. Tsiku la chisanu ndi chimodzi, kusanache [16] mchembere ilawira buli, ndi kuomba [17] ntungululu [18], ndipo mchembere zoka zoka zisonkana kunka naye [19] ku madzi. Kuti anali [20] wa chipongwe, ammanga m'mtolo, namponya m'madzi'mo. Mchembere zirikuota moto pa mtunda. Dzuwa likafunda ndiye kumbvuula namkazika pa mtunda nayamba kubvina ndi kugwedezera mutu wache ndi kumlanga, kuti, "Iwe dzimva [21], ndidakutuma kuti ukanditungire madzi ndipo udakana, ukati kuti, "Sindine muntu." Nanga ku madzi kuno udakabwera weka lero? Nanga amene akubweretsa kuno, si mchembere." Ndipo amfotokoza [22] fotokoza. Akata ammeta ku mutu ndi ku chinena ndi kumdzoza mafuta ndi kumbve ka mikanda. Ndipo ambereka pungu lache. Pamene alikunka alikuimba,

"Manya mai, manya [23],
Ndinali kwatu, ndinalije manya,
Ndadza m'Chingoni,
Ndaona manya,
Manya, eh!"

"Ziri, ziri, ziri pa ine,"

"Namwali tetera, namwali tetera,
Nditetera bwanje, ndine msoti,
Tetera."

Pofika naye ku nyumba ya mai wache aimba,

"Gubidi gubidi m'nyumba mwa mache.
M'nyumba musali mwache."

III. Ndipo ayala mpasa, nakatenga mwanna wa-

che, natambalitsa pamodzi, nayamba kummeta, tsitsi likagwa antu aponya mikanda. Atenga ndodo napingasa pa myendo pao kuti adziwe kuti ndodo imenei ndiyo idzidzandimenya. Akata kumeta, ndipo atenga mafuta ndi kudzoza [24] matupi ao. Pamene kwada mchembere zimtenga namwali'yo kunka naye m'nyumba ya mwanna wache. Ndiwo ziri pa moto. Usiku mkazi nadzukira, natenga mchere [25] natsira m'ndiwo. Mamawa, kusanache, antu asanatsegule, atenga ndiwo, nanka alikupatsa [26] amai ao ndi pungu lao. Ndiwo'zo angoika pa komo, akatsegula azipeza, napaka ku pazi ndi m'kwapa; ana ang'ono angodia. Akakala ndi abale ache, ali kutari, asongola kansungwi, natunga nyama'yo kuti wapatari uja akabwera adzapaka kupazi. Kapena wa patari akakala asadamve kuti kudagwa zotere, akabwera pa mudzi poti, "Patseni madzi ndimwe," angomkaniza dala, kwina alipo [27], nakamtusutsira [28] ndiwo kuti atsogole [29] wapaka kupazi. Kapena mkazi uja akapeza mwanna wache ndiye chimbuira, angokulungira m'nyumba momo, osaturukira kunja, kukapereka ndiwo. Ndipo mchembere zidamnyenga mwanna kuti, "Kweye ku ula [30] ukaombeze." Iye poti amuke [31], aitana mwanna wina adzata [32] unamwali. Namwali'yo akakala wopanda mwanna, mchembere zimuza kuti amuke kwa abwenzi ache; ndiko kuchita chigango [33]. Madzulo natenga mpika ni ndiwo nanka kubwalo. Amnyamata naturuka kukagona kwina. Mamawa mkazi achoka kunka kuka [34].

V

ZA CHIKUTA

I. MKAZI akatenga mimba, mchembere zikauza [1] mwanna, kuti, "Tsopano mkazi usagona nayenso mlekani matala" [2]. Mwanna, akakala ni mkazi wina, adzapita ku nyumba yache. Tsiku lomwe mkazi alikufuna kulowa m'chikuta [3], auza mwanna wache kuti, "Turukani." Ndipo mwanna uja akauza [4] mchembere, kuti, "Mkazi wanga alikudwala." Ndipo mchembere zimuka ku nyumba, ziwiri [5], nayamba kuturutsa ziwia [6] zonse za m'nyumba'mo. Mkazi'yo, akabvuta, osabala msanga, mchembere zimuza kuti, "Mwanawe [7] nena ungafe [8], kuti adakugwira wina." Kuti adamgwira [9] anena kuti, "Ine uje ndiye anandigwira." Mchembere zingobisa zimenezi. Akaona moyo [10], ndipo amsambitsa [11] mwanayo. Ndipo mchembere imodzi imuka kukauza [12] mwanna kuti, "Mkazako wachira bwino." Kapena mkazi wabala mwana wa mpongo ati, "Waona ndodo." Kuti wabala wa mkazi ati, "Waona nsengwa." Ndipo mwanna abwera, nakala m'konde napeka moto [13]. Moto omwe unali m'nyumba ataya. Mchembere itenga wa tsopano, nikoleza [14] m'nyumba. Mwanna nachoka ku nyumba kwina, sagonanso pamodzi ni mkazi wina mpaka kufikira [15] mkazache aturuka m'chikuta [16].

II. Pamene alikudziwa kuti mchombo ulikufota, mwana'yo, pomkazika pa mwendo, adzimpendeketsa [17], kuti mchombo ukaduka, udukire pa mbali; ukaduka, ukagwa pa chinena, mwana'yo adzasanduka chimbuira [18]. Mchombo akwirira m'konde. Tsiku limenelo ndilo tsiku lakumeta. Ayamba kumeta mwana, ndiye kumeta mai wache. Pakumeta mwa-

na asia tsitsi pa liwombo [19]. Mwana akakala wa kwa Maseko [20], amsia ndi pa nkongo [21], ndipo gogo amchula dzina lache kuti, "Mdzukulu wanga'yo [22] dzina lache ndi uje." Dzina loyamba adzakala nalo mpaka kufikira [23] kuseka, ndipo bambo wache, akafuna, adzamchula dzina lina. Akakulanso, adzadzichulira yeka, kuti, "Tsopano ndine uje." Akakula nditu, adzasianso dzina lache la kale, ndi kuchula [24] lina. Muntu akamchula dzina la kale, ati, "Wandichula dzina la chinkumbangaluwe." Pamene ameta ata [25], gogo wache akhala [26] mankwala, dzina lache pfundabwe, asanganiza ndi mafuta a nsatsi, ndi chikule, ndipo kupaka [27] pa liwombo [19]. Mankwala ameneo apaka masiku onse. Mwana akakwima ndiye kuleka. Pamene apaka [28] mankwala, aopetsa dzuwa, kuti lingabōle pam'tu. Ndiponso atenga chizuzu natsira m'dende wopikira bota. Kudzaleka bota'lo koma mwana'yo atakwima [29].

III. Tsopano nayamba kufukiza [30] mwana. Atenga muzu wa nyalinse ndi mayani [31] a chipunganyunyu naika m'ntalo [32] ya madzi, natenga miyala ya nsangalabwe [33] inai, naika pa moto, ikapsya napana, natsotsoloza [34] m'madzi, mtunzi [35] imgwira mwana'yo. Pamene atero [36] aopetsa tsempo ndi mauka [37]. Ndipo azira m'nyumba, natenta zintu zomwe zidatsala [38] m'nyumba'mo, nsengwa ndi pale, ndi zipande. Moto afumulira pa mtunda [39], aola fulusa loka, pommanga mwana mkuzi, azima moto [40], akapala ku nyumba yina. Ndipo abwera mwanna, naimirira [41] pa komo, namtema mwendo. Ayambira chala chachikulu, natema mphini zinai pa nsongolo zinai, pa bondo zinai, mbali yina ndi yina, mwendo winanso chimodzi modzi, pa chifuwa atema mphini ziwiri pa msana ziwiri. M'mphini'zo apaka mankwala a chinyalo [42]. Pamene atero, aopetsa, akalumpa pamene akakwirira mchombo ndi nsapo [43], angatenge ntenda ya mwendo. Mwanna uja akakala ndi mka-

zi wina, ameneyu ndiye apota mkuzi wa chingwe cha mpoza, ndiye kuika pansi pa mpasa pomwe agona. M'mawa mwache nalawira kukamanga mwana'yo mkuzi. Muntu'yo akakala alibe mkazi wina ammanga mwana ndiye mbale wache. Mwanna saona nkope ya mwana wache msanga; koma tsiku lina mchembere zomwe, ndizo zimgwiritsa m'manja. Bambo [44] uja nakoka chira [45] la mkanda napatsa mchembere.

IV. Pamene aona kuti mwana wayamba kumera mano a kumsi ndi kusekera antu, akulu amuza bambo wache, kuti, "Tsopano ubweze mwana m'mudzi." Gogo wache wa mwana akungiratu [46] lizango. Ayamba ni kansaru nakulungakulunga [47] mankwala pamodzi ndi chingwe; ndiye kutenga kanguo asokezerà pompo, natenga mikanda narukira pompo. Mkazi napikiratu ndiwo [48]. Madzulo ache mkazi ndi mwanna agona pamodzi, (ndiko kubweza mwanna m'mudzi). Adula mkuzi wa kale, ammanga lizango, lizango lina amtsamiritsa mwana ku mutu. M'mawa natenga ndiwo kukapatsa mchembere ziwiri zija, natenga lizango lomwe anamtsamiritsa, namanga pa kosi, ndipo atenga mkuzi wa mikanda apakiza mpinjiri, nambveka mwana'yo. Lizango likaduka, salifunafuna, angoleka. Mwana wa kanda akafa, asanambweze m'mudzi, akataya ku dambo m'pepete mwa'madzi, maliro ache alira akazi oka. Amuna akaponda pamenepo, watenga ntenda ya nyesi. Dzina la manda ndi nsenye.

VI

ZA MASASA

I. MFUMU wa pa mudzi, pamene alikufuna kututa masasa [1] auziratu amnyamata [2], kuti afuniretu mirimo, adzingounjika [3]. Ndipo tsiku lina mkulu alawira kunka alikuyang'ana [4] mbuto yabwino. Akaona [5] kuti mpabwino, ati, "Malo anga ndi ano." Akanka ku mudzi, madzulo ache [6] auza antu ache kuti, "Musasimbwa [7], ndirikufuna kuti ndikakolekze [8] moto pa tengo, pano pandikhola" [9]. M'mawa kutacha [10], mfumu ilawira ndi mbale wache, ndi sing'anga, ndiye kunka [11] ku masasa. Ayamba kuzungulira, alikumanga dzikosi [12], napaka mankwala, napeka moto [13] pamene alikufuna kumanga nyumba ya kuka [14], natsira mankwala pa moto'po, natenga madzi napemerera. Pamene atsirika [15] choincho aopa mfiti ndi mikango. Ndipo antu akumudzi kumabwera ndi mirimo, nāuza kuti, "Lambulani apa." Nalambula, akata, mwini wache wa pa mudzi atenga nsichi za pa komo, nazika, akazikanso za pa tala, antu a chabe, ndiye kuziika. Akata kumanga ya kuka, ndiye kumanga ya mulumuzana [16]. Kukada antu ena ndiye kuchoka kunka ku bwinja. Apo patsala mfumu yoka ndi antu ena amene agona ku masasa'o, sadzabweranso kukagona ku bwinja. Madzulo ache natenga moto kukakoleza m'nyumba, pokoleza sakala pansi, akoleza chachiriri; pamene atero, aopetsa utsi, kuti ungamadzabvulungane [17]. Antu a akazi adzingobwera [18] masiku onse kudzapika [19].

II. Pamene ata nyumba za mafumu ayamba kumanga za ndota, [20] zikata izo, ndiye kutenga nyumba zonse. Akaona kuti zinyumba zonse zata, apika moa ku bwinja, nakatenga mizimu [21]. Yemwe ali

ndi litinda [22] atsira moa m'dende [23], akakazika pa manda nanena kuti, "Pano tachokachoka musafunafuna, tiyeni tinkire limodzi" [24]. Tsiku limenelo ndilo agwetsa nyumba zonse zomwe zitsala, asia nyumba zoka za masiye. Poti pano dzuwa lapendeka, kuka [25] atenga madende asanu, natsira moa, ndiye kutsogoza atsikana osenza madende. Mwini wache mchembere ya kuka ikala patsogolo, mkazi wa mfumu wamkulu, ndiye atsata gogo, a moa amadza pambuyo. Akafika pa masasa, atuza madende ndipo antu onse asonkana, mkulu wa pa mudzi nayamba kukusula [26], kuti, "Nao moa [27], tapika ife pansi pano, kunja tidachoka, lero mudzi wanu nao [28], antu onse mudzayang'anira bwino." Ndipo mwini wa pa mudzi akoka mbuzi [29] napatsa mkulu'yo, mkulu'yo nanenanso kuti, "Nayi [30] mbuzi yomwe akoka mwana wako, mudzimwerera moa" [31]. Ikakodza, ndiko kuti [32] mzimu walola, [33] ikaleka [34] ku kodza, sapa'i. Ndipo apa mbuzi'yo natenga chiwindi [35] ndi mapapo, ndi tumbo, ndi kukazika pomwe pali moa, nadula nyama ya mwendo wa m'mwamba, naocha, nadula apatsa gogo wa kuka, nadula yina, apatsa bambo wa pa mudzi, yina adia ndota yache, ndipo ayamba kudulira [36] ana ao. Nyama yina angoika m'dengu, m'mawa mwache [37] adzasasira nyama yonse.

III. Akata kukusula mkulu wa pa mudzi auza ndota yache kuti, "Lero upike ndiwo, upatse antu onse, ulongose masasa." Iye nagona ni mkazache, m'mawa mwache natenga ndiwo kukapatsa mfumu [38]. Antu onse a chabe amadzatengera ku nyumba konko, yemwe ali patari amwiika zache. Tsopano masasa ata, yemwe amene afuna kugona ni mkazache angogona. Akala mwezi umodzi ndiye kupika moa wambiri pa mudzi ponse'po ndi kubvina chamba [39], kuti pa m'dzi pafumbire [40]. Akagonanso, apika moa wogwetsera nyumba za masiye zimene

zidatsala pa bwinja'po. Pa masasa'po pakadzafa muntu [41], woyamba akamtaya ku bwinja, akadzafa mkulu amtaya pa masasa pompo, ndipo antu onse amene adzifa [42], adziwataya [43] pa masasa.

VII

ZA ULOKAZI

I. NGONI akakala [1] ndi ana ache a akazi, apangana [2] ndi muntu wa pa mudzi wina kuti, "Iwe ndiwe bwenzi langa [3], ukwate [4] mwana wanga." Ndipo bambo [5] uja wa mwana apika moa, nakaitana [6] bwenzi lache, nampisa m'nyumba ya yeka [7], nauza ana a akazi kuti, "Mudzikamtsirira moa [8] mlendo'yo." Bambo uja asonyeza mwana wache, kuti, "Udzaona wobvala nsaru yakuti [9], udzadziwa kuti ndi yemwe'yo." Ndipo tsiku lina auza mwana wache kuti, "Kadire [10] kwa uje," Mwezi ukawala asonkana atsikana [11], ndipo usiku afika pa mudzi pa mwanna, nakala pa bwalo, angozungulira, mlokazi akala pakati, nsaru zao afunda ku mutu, gudu! gudu! Akamba nkani zao, alikuseka kuti eni a pa mudzi adziwe kuti kwabera antu ku bwalo'ko. Ndipo mnyamata mmodzi aturuka nati, "Ndiyapeya" [12], (ndatola). Mzache nati, "Ndiri nawe." Ndipo mkulu afunsa kuti, "Kodi n'chiani." Ndipo iwo ati, "Kwadza mitimba" [13]. Ndipo auza atsikana a pa mudzi kuti, "Takafunsani [14] antu ali ku bwalo'ko. chimene adzera" [15]. Ndipo afunsa kuti, "Mwatsatanje kuno?" Ndipo iwo ati, "Tatsata uje," Alikuchula kamwana kakang'ono. Ndipo afunsanso kuti, "Kodi mulikunena mwana iye, iye'o" [16]. Ndipo

iwo aja ati, "Iai koma tirikunena mkulu wache." Ndipo akauza akulu kuti, "Antu aja abwera ku bwalo'ko, alikuti afuna uje." Ndipo akulu ati, "Kapiseni m'nyumba." M'mawa mwache [17] nāpikira [18] ntakula [19], mlokazi uja sadia nao, mchembere zikaona alikufa ni njala [20], amtenga, kunka naye [21] ku nyumba ya ku mapeto [22], nakampatsa moa.

II. M'mawa mwache a pa mudzi wa mwanna akoka mbuzi [23], kapena ziwiri, kunka nazo ku mudzi wa mkazi. Mbuzi'zo angolandira ati, "Izi n'za mzimu, malowolo akale [24] pambuyo." Ndipo pochoka, ayeni [25] asia mwana wolonda mkazi'yo, akafika kwao, atenga mbuzi zina, nankanso nazo, akafika pa mudzi wa mkazi, angokala pa bwalo, mkulu wa pa mudzi ang'amba mpanda, nasuzumira [26]. Akaziona mbuzi'zo auza mwini mudzi kuti, Taziona, ziri mwakuti" [27]. Ndipo mwini wache wa pa m'dzi ati, "Musalandira'i." Ayeni aja akakala kala, nachoka kunka kwao, ku nkutu, naima kudikira alokazi, nakauza mwini wache kuti, "Sanatilandire." M'mawa mwache natenga mbuzi zina, nanka nazo. Mkulu uja ayang'ananso, akaona kuti zabwera zina, auza mwini wache wa mwana kuti, "Lero zabwera mwakuti." Mwini wache uja ati, "Kazitengeni mwiike mkola." Ndipo abwera mkulu, atenga ndodo ya mwiyeni wamkulu, nakaika m'nyumba ayeni aja natsata ndodo, nāpikira nsima [28], nakana, nabaisa [29] mbuzi, nadia. M'mawa mwache amuka kwao. A pa mudzi wa mkazi ati, "Mudzionera ife" [30]. Kuti chimera chinali [31] chonyika, sagonetsa masiku ambiri, kuti chinali chosanyika [32] agona mwezi umodzi. Tsiku losuza [33] moa, akaitana ayeni, nabwera ndi mwanna yemwe kudzamwa [34] moa. Mwini wa mkazi akampisa ku nyumba ya ku mapeto, awiri ni mkazache [35]. Moa wao adziaturutsira kankali kakang'ono.

III. Ndipo antu onse asonkana pa bwalo, natenga mbuzi. Mlokazi akala pa mpasa. Gogo wache[36] ammeta chipumu[37]. Akata kumeta, aturuka myiyeni, nayamba kupa mbuzi. Mbuzi ikaleka kufa msanga, ammenya. Ndipo ayamba kusenda, atenga nyongo, ndiye kumdontozera pa m'tu pache pa mlokazi, nabvutira nyongo zonse. Atenga miseso[38], nayanika ku dzuwa, nakatsa bwino. Madzulo namtenga mkazi'yo kunka naye kuka, napukusa chitundu, nasamba mlokazi'yo, abwera mwana uja wolonda, nasambanso, ndiye kutenga nyongo ndi miseso, nyongo namangirira m'mutu, miseso namkupatiritsa m'kwapa. Mwana uja akammangirira akata[39], ndiye kummenya ayeni. Ndipo anyamuka mkulu wa pa mudzi kuti, "Nayo mai wanu[40], tanipatsa[41] lero, ndipo alibe ntenda yina, ntenda yache ndi litsipa[42], akakachita tsempo[43], koma kwanu, kuno kulibe tsempo." Pamenepo ndipo kunyamuka ayeni onse ndi anamwali a pa mudzi'po, kukapereka mbale wao. Popita mlokazi ambereka. Pamene afika pa mudzi pa mwanna āpisa m'nyumba momwe adafikira poyamba. Mlokazi agona m'nyumba'mo pamodzi ndi anzache. Mawa zituruka mchembere zinai, ziwiri za kwa mkazi, ziwirinso za pa mudzi wa mwanna, nåtenga mlokazi kunka naye kuseri. Akaona kuti ziripo[44], abwera, alikuimba nkulungwani[45], alikuti, "Ng'ombe ziripo, ng'ombe ziripo." Akaona kuti ng'ombe zidata, bambo wa mwana adzabweza mbuzi ziwiri, kapena zitatu, akafuna angoti, "Metereni wina." Ku chitangamire[46] abvina nsindo[47]. Ndipo achoka kunka ku bwalo, kuti akakaye[48] pa maso pa antu onse. Akakaya, aturuka mwana uja, nalanda ndodo, mlokazi nagwada pansi, mwana natenga lichero, nayamba ku bvula nyongo ndi miseso, akaika kuka. Atenga nsaru nambveka nanka naye ku nyumba ya mwanna wache. Madzulo nadula nkwindi[49] nasia pa

mpasa pompo. M'mawa mwache mkazi atenga mtsuko, nakatunga madzi akazira m'nyumba ya kuka. Mchembere idzatenga nkwindi nakaika pomwe pali nyongo ndi miseso. Akakalitsa ndiye kumpikitsa moa. Tsiku lakumwa moa atenga nyongo natenta, nkwindi napulula, natunga mwini wache zipote.

VIII

ZA UKWATI

I. Mkazi ndi mwanna akakondana [1], adzingopatsana [2] zao kuseri, ndipo akakalitsa [3] ati, "Koma ziululuke zimveke [4] ku antu." Ndipo mwanna uja akauza [5] akulu akwao kuti, "Takandifunsirani [6] kwa uje ndifuna kuti ndidzikala nao, ndasauka ndine." Ndipo akulu amuka kukamfunsira kuti, "Pano taona nsengwa [7], tirikuti tikale nanu, tasauka ndife." Ndipo mwini wa pa mudzi ati, "Tsogolani mwati pambuyo [8], ife tidakafunsa ana a panga pano, akadawira [9], mudzamvanso." Ndipo aja amuka kwao. Mkulu uja naitana ana ache, naona mwana yemwe wachenjera [10], namfunsa kuti, "Pano panadza auje, ati alikufuna iwe kuti udzakale nao" [11]. Ndipo mwana uja ati, "Nanga ine ndine nditani, mau amene munganene inu, ndibvomera." Ndipo abweranso antu aja a kwa mwanna, nati, "Tabwerera yomwe ija [12], tidanena dzulo, ife tifunitsa nditu," Ndipo bambo uja ati, "Mwana'yo abwere [13], adzakale pompano, ine sindimkana'i." Ndipo aja abwerera kwao, nakamuza mwanna kuti, "Kuja tinanka, ndipo takamva zomwe atiuza, ati mukakale konko."

Ndipo mwanna uja ati, "Tikakala, kuli madzi sikulikutari." Ndipo akulu aja abweranso komwe nakati, "Tikala nanu konkuno, taonani kuli madzi sikulikutari." Ndipo bambo wa pa mudzi ati, "Ngabwere [14] kulibe kwina kodia muntu." Ndipo akulu aja abweranso nakamtenga mwana wao, nafika naye pa bambo uja, nati, "Nayu muntu wanu [15], koma ameneyu alibe mau ena, mau ache mbakuti [16], "Pikireni [17] nsima, ine ndine ni njala." Bambo wa pa m'dzi nati, "Nafenso [18] watu'yu alibe kantu kena, kupika n'kwache, kusinja n'kwache [19], nyalo [20] kulima, momwe tisanaone pogwira kasu lache" [21].

II. Ndipo akulu aja abwerera kunka kwao [22], mwana uja namsia, amangogona m'bwalo [23] mwa ana, mkazi wache adzingompikira nsima osagona [24] naye, kufikira [25] kumanga nyumba yache. Akata kumanga ndipo ampisira. Pamene alikukala pa mudzi 'po, osamaonana ndi mpongozi wache [26], adzingotawana masiku onse. Akati, "Kutawa kwandikhola [27] tsopano koma tifundulane." Ndipo mpongozi wache apika moa, nkamwini natenga nsaru, nakaitana antu a ku mudzi wa mwanna kuti, "Tsopano tirikufuna kuti tifundulane." Ndipo antu a ku mudzi kwa mwanna abwera, ndiye kutenga [28] mwanna'yo, nanka naye m'nyumba mwa mpongozi wache, nsaru yache iri chifundire [29] ku mutu, mpongozi wache, nayenso iri chifundire. Ndipo mbale wache wa mwanna akafundula [30] nsaru ya mpongozi, natenga chira napereka kwa mpongozi. Mpongozi natsira nkali ya moa nakapatsa mpongozi wache wang'ono, namwa imwa [31], nalandizana pompo. Mbale wache uja ali chigonere. Akata, ndiye kuturuka mpongozi wa mkazi, mwanna uja nadzuka nayamba kumwa nao moa anzache, nati, "Tsopano chipongozi tafundulana tata" [32] Adzingochitana ulemu woka.

IX

ZA KACHISI

I. MVULA ikakana [1], antu ati, "Taonani mvula yakanirira kumwamba, tiyeni tikayesere [2] kukusula [3], kapena mvula ingabwere." Ndipo ayamba kupangana kuti, "Nonse inu musonke chimera m'manja m'manja [4], tikangoyesera, dzikakatichimwa, dzikatichimwire pompo" [5]. Ndipo ayamba kusonka chimera, lero lomwe naperatu, ndi kusinja [6], napika, natsira m'dende. M'mawa mwache [7], kutacha [8], asonkana antu onse, nanka ku kachisi. Alambuliratu, kuti payere pansi. Mwini wache wa kukusula akala pakati, nayamba kutunga moa, namatsira m'nkali yokumbira pansi nati, "Mbuye Chauta [9] watumira [10] mtima, wati ife titani, tipasuke [11] nditu. Mutipatsa ife mvula ana anu, nao msunje [12] tirikunipatsa [13] inu." Ndipo antu onse ayamba kuomba m'manja ndi kuimba nkulungwani [14], alikuimba, alikugadama namati, "Pepa, pepa" [15]. Akata kukusula atunga moa omwe watsala, natunga m'chiko, namanka alikumwetsa [16] antu onse pang'ono pang'ono, osaoneka wina woperewedwa, ndi ana omwe awalawitsa pang'ono pang'ono. Akata atenga matsamvu a mitengo nayamba kubvina alikuimba nyimbo nati—

"Kantambo ndi aka ndi aka,
Kadze mvula ndi aka,
Patseni madzi,
Ku mtima kwauma,
Krole,
Patseni madzi,
Ku mtima kwauma,
Krole."

Akafika ku mudzi, afeza mchembere yatungiratu madzi, niika pa komo, antu nayamba kunyika [17] matsamvu·ao, nawaza kumwamba, alikuwaza alikuti psya! psya! ndipo aona mvula iri tsitu! tsitu! tsitu! [18]

X

ZA ULA

I. MUNTU akadwala [1] ndipo mzache anka alikufuna [2] ula [3]. Afikira panja nati, "Zikomo" [4]. Mwini wache ati, "E pitani momuno" [5]. Ndipo iye alowa m'nyumba'mo nati, "Tadzera inu kuti mungatilondere [6] mzimu." Ndipo iye aturutsa ula wache m'tumba la likongwe, natenga fulusa, napakapaka ula wache, nayamba kuombeza nati, "Kodi mwadwaza?" [7] Ndipo iye abvomera kuti, "Inde, ndadwaza, kalikudwala n'kamwana [8], sindirikugona naye tulo, ndi bota lomwe salikudia'i, ndipo ndati koma ndimuke [9] ku dzisolo [10] (ula), kapena kumenemwana'yo." Ndipo iye ayamba ku ombeza nati, "Pali mzimu wa gogo [11] wache, ndi'wo ulikudwalitsa mwana'yo." Mwini wache amene wadzera kunjira'yo ati, "Ndiyabvuma" [12]. Ula unenabe kuti, "Bwanji musalikundikumbuka, ndi mdzukulu [13] wanga yemwe, ndiwe udzipanda kundikumbuka." Koma mzimu'o mukakaupatsa nkuku mundionera [14], mwana'yo alikukala tsonga, mukakatenga nkuku'yo mukagwade nayo pansi, mukati, "Gogo nayo nkuku [15] imene ulikutengera muntu" [16]. Ndipo muntu amene wadzera ku njira'yo ati, "Mutiikire mzimu watu m'tumba."

II. Ndipo iye amuka kwao natenga nkuku yache

nagwada nayo pansi, natenga chiko cha madzi, nabvumata, napemerera, nati, " Gogo, nayo nkuku imene ulikudwalitsira muntu; uchita kuuma mtima chifukwa nkuku yoka yoka; kaleke kanterera [17] kako, nakonso kadzienda [18] ngati [19] chomwe alikuchita anzache; musaonera'po [20] poti mutengere muntu [21] nkuku yoka." Ndipo atenga nkuku napa, nasosola, natumbula, naocha dziwindi [22], naika ku mitu [23]. Nyama ikapsya, apika nsima, napakulirapakulira m'zinsengwa, ina nasia m'nkali, nayamba kukusula nayo nati, " Nayo nkuku yanu tanipera: [24] mudiera pamodzi, pasaoneka wina woderera. Nayo nanunso ana ang'ono, mudzidiera pamodzi ndi kukondwa " [25]. Natenga nkali 'yo nati, " Iyi ndiyo ya inu, mchembere zazikuluzikulu." Ndipo akata kukusula [26] atenga nsima nakaika ku mitu, yoti adzadie m'mawa yatsala'yo, nayamba kugawira antu. " Inu nayo yanu, inunso nayo yanu, mchembere, yao, nai." Akata kudia ayamba kuomba m'manja, ndi kuimba ntungululu [27], ndipo kubalalika. M'mawa mwache [28] pamene kwacha atenga imene anaika ku mitu, nadia [29].

XI

ZA UZIMBA

I. Muntu akafuna [1] kumema [2] uzimba [3], auza anyamata kuti, " Pitani mulikumema [4] uzimba, antu'o mudzikauza [5] kuti ulowera kwa kuti [6], ndiko [7] tidzikasonkanirana." Ndipo amnyamata atenga ndodo, amanka alikumenya ndodo, amaimba nyimbo

amati, " Wo, wo, wocha, wo, wo, wocha." Akafika pa mudzi, eni ache a pa m'dzi ati, " Ocha," nafunsa, " M'bwaani?" [8] Ati, " M'bwauje, ulowera kwa kuti, antu onse adzikasonkanisana kumeneko." M'mawa mwache [9] pamene kwacha, ayamba kusonkana, akola agaru ao [10], natenga ndodo ni mikondo [11], natsogoza [12] kamwana, ali [13], " Kumata " [14]. Pofika ponikira [15] uzimba amuza mwana'yo kuti," Gona apa musamatakataka." Ndipo antu onse amene alikubwera amatenga masamba amamkundikira mwana'yo. Kumeneko ndiko kuti nyama zisamakachenjera. Ndipo mwini wache ayamba kubulanga kuti, " Taonani, ena ali ndi agaru ao, mudziyang'anitsa mabanga ao." Nayamba kubunika, nati, " Lipondo [16] la kwa uje lilowe apa, la kwa ujenso lilowe apa, eni ache pakati." Namanka alikuwamba [17]. Nyama ikauka, wina akaibaia, mzache akabwereza [18] ndi msomole [19]. Amene wayamba kuponya, nkana [20] atangolasa [21] pang'ono pang'ono, mzache akaitsiriza, nyama nja yemwe [22] wayamba.

II. Ikakala nyama yozengerana [23], alikuti, " Wayamba ndi garu wanga " [24], wina, " Wayamba ndi garu wanga," ndipo ati, " Tiyeni tikumbe mankwala." Ndipo atenga mankwala'yo muntu wina ache, wina ache, atafuna, napemerera garu wache nati, " Garu iwe, usali iwe [25] ufe, kuti uli iwe usanze." Winanso anena chokachokacho [26], ndipo aona wa wina alikufa. Akakala antu akaponya pamodzi, wina alikuti, " Ndayamba nd'ine," ati, " Tisamangosautsana, tiye tipite kwa sing'anga." Samwa oka, amwa ndi agaru ao. Akata kusaka ati, " Ngābuguduke [27] tsopano." Nyama zonse aunjika pamodzi, mwini wache wa uzimba ayamba kukumula myendo yache. Akaona nyama yachuruka, awenga wenga mizongo, nachitira utao, nakolozera moto kuti iume. Ikauma, ndiye kukungula, namanga m'mtolo.

III. Uzimba wina wa antu ambiri ndi agaru ao,

wina wa mlenje. Ena akumba mbuna nachita chinga, amasia mipata mipata momwe wakumba mbu na'mo. Uzimba wina wa chire lodulira. Muntu adulira chire lache, machire onse akapsya, litsala loka'lo. Nyama zitawa poyera [28] zimadzalowa m'chire lodulira'lo; poti tsopano mvula irikuyamba kugwa, ndiye kukatenta chire lodulira'lo. Nyama zimatawira poyera, antu amazipera. Nsampa wa njobvu ndi chera. Achera m'nkwaso momwe zipita njobvu. Atenga chera, amangirira mwamba, matanda ache nakala pansi. Njobvu, popita, idzakukulula matanda'o, chera chitsekuka, chigwa pa msana pa njobvu. Antu asakanso ndi ukonde wa nyama: andandalitsa ukonde, natenga chikomo, nakoma ku mapeto, china pakati. Antu natsala, alikusaka mbuyo muno, nyama ikauka, ikalowa mu'ukonde. Mbalame antu asaka ndi ukonde wong'ono, apanga ndi mabango awiri, nagwira m'manja, nakalira. Ena apita kukasaka, mbalame zikalowa pa ukonde, nazunguza, natsina pa mtima, zingalire, naomba mluzu, osaka naima. Mbalame zimene antu asaka ndi ukonde, maina ao, Mpeta, Madzanjo, Atii, Napwiti, Kuzikuzi. Nkwali, Nkanga, Mang'ani, Njiwa asaka ni ndodo, pamene ziuluka aponya. Mbalame asakanso ni nyankwa, zinanso achera ni nsampa. Nyengo yachirimwe, madzi akatsala pang'ono, ndipo mbalame zonse za ludzu zipita kukamwa madzi, zizolowera pa madzi'po. Muntu akaona kuti ziri kumwera madzi apa, nayamba kuchera ulimbo [29]. Amata ku mtengo, nazika pa madzi, mbalame zikafika kudzamwa madzi zimatidwa myendo ndi ntenga zomwe. Antu asakanso mbewa. Mende, ndi nchenzi, ndi sakwi, asaka ndi magoba [30] (madeka), achera pa mleka [31]. Ena antu nakasaka, wina nadikira, poti itawe, nilowa m'goba, atsina, nakutula. Acheranso ndi diwa, ni nsampa, zina achita kukumba, ndi kufukiza. Mbewa zifula una, patsogolo pache zichita

pfunka, m'funka ziika masa, patsogolo pachenso ziika kambuli konenekezi, kuti muntu akakumba, iyo idzangobulikira pompo. Zina mbewa zimanga chisa pa udzu. Siswiri sadia antu, sangalumpe njiri, akayesa kulumpa, afa.

XII

ZA MABISALIRA

I. MUNTU pamene wafa, mwini wache wa maliro amuka kukafuna [1] mabisalira. Akampeza, amuza kuti, " Kwatu kwagwa zoipa, ndirikuti kapena mukandilondere [2] chimene chapa muntu." Mabisalira abwera madzulodzulo [3]. Akabwera, ndipo mwini wache wa maliro ampatsa ana kuti akamperekeze ku manda'ko. Pamene afika pa manda'po, afunsa kuti, " Anadzera nao kuti mtembo?" Ndipo anena kuti, adzera [4] apa. Ndipo ayamba kutsirika pomwe anadzera'po, nafunsanso kuti, " Nanga mutu wache waloza kuti?" Ndipo ati, " Mutu wache aloza uko." Natsirikanso kumeneko. Ndipo mabisalira apeka moto [5], nakoleza, natsira mankwala; pamene [6] atsira mankwala aopetsa kuti angadzaone moto. Ndipo aona mfiti zirinkubwera; ziima kutari, ndipo ziitana muntu wakufa'yo, dzina lache la kale, lobadwa nalo [7], nati, " Uje turuka." Ndipo ayamba kuturuka. Ndipo mabisalira ati, " Usaturuka, ine ndine malombolo [8] wako." Ndipo iye abwerera [9] pansi'po. Mfiti zija ziitananso, nafuna kuturuka, mabisalira nanena chokachokacho [10]. Ndipo mfiti zinena kuti, " Kodi nd'ani amene alikukanizira nyama yatu?"

Ńaponya mpinjiri ziwiri zisanduka mikango, imabwera, irikupalasa ndi kubangula [11], ndipo mabisalira aona zirikufika pafupi natenga mankwala ache, nawaza, ndipo zirombo zija zisanduka mpinjiri, natenga mpinjiri'zo, naika m'nyanga mwache. Atumiza zirombo zonse, zilepera. Ndipo ati, "Nd'ani ani [12] amene alikupambana ife, tiyeni, tiyeni, tiyeni tikamuwone" [13]. Ndipo abwera poteropo [14], ndandanda, natuma mmodzi, ali [15], "Tanka iwe ukadule m'chuuno." Ndipo poti ayambe kudula m'chuuno, osata'i nabwera nati, "Iai, iai, iai, sindirikuta kudula." (Mabisalira ndi moto wache ali ga!) "Ngānke [16] wina akayese, kuti mulikuyesa [17] kuti ndirikunama." Ndipo wina'yo, poti akadule, akachimwidwa chokachokacho [18]. Ndipo mabisalira ati, "Tatopa nao." Natenga mchira wache nawaza, wa! nafa, ndipo ayamba kwazindikira kuti, "Uyu ndi uje, uyu ndi uje." Ndipo mabisalira afunsa kuti, "Kodi nanga tiwatani, nanga tiwape, kapena tiwaleke?" Ndipo kapena mwini wache ati, "Apeni." Mabisalira natenga dzisonga dzache nayamba kwapisa ku mpeto nayamba mmodzi mmodzi, namuza kuti, "Iwe, uswere masiku atatu, la chinai udzafe;" nauzanso wina, "Iwe, uswere masiku anai, la chisanu ufe." Onse nawanena chokachokacho. Ndipo atenga mankwala ena nawaza, ndipo kudzuka, nayamba kutawa, nayenso mabisalira natawa. Kumudzi akagona masiku atatu amva kuti uje wafa, ogona masiku anai amva kuti uje.

XIII

ZA KUKUSULA KWA ANGONI

I. PAMENE ikana mvula, anka pa ula [1] kukaombeza [2]. Waula anena kuti, "Pali mzimu waukulu ndiwo ulikukanitsa mvula." Ndipo akulu akulu onse asonkana. M'mawa mwache pamene kwacha aturutsa ng'ombe m'kola, mfumu niimirira niti [3], "Ng'ombe iyi ndapatsa inu, Gogo [4], kutu inu ndinu mulikukanitsa mvula; mutipatsire ife mvula ana anu; taonani antu onse alikusauka chifukwa cha inu." Ndipo akulu abvomereza kuti, "Yewo inkosi mutilekerani, titangate ife antu ako." Pamene alikubvomereza antu, ng'ombe ikodza ndipo antu ati mzimu wabvuma [5]. Ikaleka kukodza ali, mzimu wakana, naileka ng'ombe'yo, napitanso pa ula. Napa, nadula mchira, naika m'nsengwa, natenganso chiwindi [6] naika m'nsengwa momo, anka nazo kuka [7], nakakazika ku mitu [8], ati, "Nayo [9] ng'ombe yanu tanipera." Ndipo atenga nyama yonse nakaika m'kuka. M'mawa akulu alawira kukasasira, antu onse adia.

XIV

ZA MALIRO A ASUTU

I. MFUMU ya Asutu [1] ikafa [2] sauziratu antu, ābisira kuti angatawe amnyamata. Tsiku lonena, agwiriratu amnyamata ndi anamwali ndipo akauza antu

onse kuti mfumu yafa. Ndipo asonkana antu onse kunka ku manda [3] nakumba kumba mudzi [4] waukulu. Akaona kuti mudzi wata, atenga amnyamata ndi anamwali nametameta, nadzoza mafuta diululi! chikule pi! Amuna agwiritsa mauta ao m'manja ngati [5] alinkunka ku masewera kwina [6] alikufa. Ndipo anyamula mtembo, amnyamata'o natsogoza patsogolo, mtembo umatsatira pambuyo. Akafika pa mpambano atenga mnyamata mmodzi nasongola nsungwi namkomerera pa m'tu ndi mwala, ndipo chikomo chiluma pansi. Angokala tsonga, ngati ali moyo, uta amgwiritsa m'manja. Pamene afika pa manda nayamba kuchola ena'o myendo, natira madzi a sabola ku mitu. (Pamene atero [7] aopetsa kuti abale ao angadzafukule kuti angakaikirire dziko lina). Naponya kutsogolo kwa mudzi natenga mtembo natsamiritsa. Ndipo akwirira, antu a moyo'o alikungolira, "Maio! maio!" Akata kukwirira anka kumadzi kukasamba. Pobwera ku madzi'ko ayamba kubvina chamba [8].

XV

MFUMU YA KUKA NDI MKAMWINI

I. Mfumu ya kuka [1] ndi mkamwini [2] wache adalima m'munda. Pamene chimanga chidakula mpongozi [3] adauza mkamwini wache kuti amange nsanja [4]. Ndipo mpongozi wache anakasulitsa [5] mibvi, napatsa [6] mkamwini wache, kuti, "Mibvi nai [7] mudziyang'anira [8] nayo m'munda muno." Ndipo mkamwini uja analandira mibvi, namagona ku nsanja konko. Tsiku lina kudadza mpepo, niwanda

wanda [9] chimanga, ndipo mpongozi wache anabwera kudzaendera [10] m'munda'mo, ndipo anaona mpepo yawandawanda chimanga, naomba m'manja pi! "Ho ine, ndiona maere, mibvi ija ndidangosula kuti adzingokala nayo." Ndipo ananka pa nsanja pomwe panali mkamwini wache, nafunsa kuti, "Kodi mibvi ija ndidasula, ndidangosulira kuti mudzingogona nayo pa nsanja pano." Ndipo mkamwini anati, "Kodi nanga n'kulasa [11] bwanji mpepo?"

II. Pamene anachoka mpongozi uja, mkamwini anatenga chimanga chache nanka kukachera maliwa, ndipo diwa lache linagwira nkanga, naonjola, nakapatsa mkazache kuti, "Nayo nkanga [12], mupike, ine ndirikunka kutari, ndikagona masiku anai, ine mudzandiwambire msuze, nyama mudia noka." Ndipo mkazi uja anakauza bambo wache kuti, "Antu aja apa [13] nkanga yao, alikuti muwambire msuze, nyama mudie, kumene alinkunka akagona masiku anai." Ndipo bambo uja anati, "Msuze nduwambe [14] bwanji mwananga?"

III. Pamene mkamwini uja anabwera anauza mkazi wache kuti, "Pika nsima." Ndipo mkazi uja anapika nanka nayo kwa mwanna wache. Koma mwanna uja anayang'ana m'mbale nati, "Kodi msuze wanga ulikuti, uja ndinakuuzani inu kuti muwambe." Ndipo mkazi uja anakauza bambo wache kuti, "Alikufunsa msuze." Ndipo bambo uja anakauza antu kuti, "Kuno mudzandiweruze." Ndipo antu anasonkana pa bwalo bi, nati, "Mfumu ya kuka tautandani mlandu timve." Ndipo mfumu ya kuka anagwira moyo [15], nayamba kulankula kuti, "Ine ndirikuti mutandifunsira [16] mkamwini wanga'yo zomwe ziri ku mtima kwache." Ndipo antu aja anaugwira naupatsira mkamwini. Ndipo mkamwini anati, "Inde zimenezi alikunena'zi n'za ine, koma ine ndinali pa nsanja, ndipo ndinaona mfumu ya kuka alikundifunsira kuti, Kodi iwe ungogona pa

nsanja pano osayang'anira m'munda, mibvi ndidakasulira kuti udzikala [17] nayo osamayang'ana [18] zomwe zirikudia m'munda." Ndipo, ine ndidati, "Kodi inu mpepo n'kuilasa bwanji? Ndipo nanenso [19] ndidakagwira nyama yanga kuti naonso andiwambire msuze, kuti iwo adziwa kulasa mpepo, ine nanenso andiikire msuze; idatero mirandu yache." Ndipo akulu anati, "Kodi mirandu yache njimeneyu, adalakwa mfumu ya kuka."

XVI

KAMBA NDI GWAPE

I. ADAPIKANA makani ndi Kamba ndi Gwape [1]. Gwape adati, "Kodi Kamba, ungate kutamanga pamodzi ndi ine?" Kamba adadawira [2], kuti, "E ndita." Ndipo Kamba adanka kukauza [3] anzache kuti, "Ife tapikana makani ndi Gwape, alikuti titamangire [4] pamodzi ndipo inu anzanga tiyeni mukanditandize." Kamba nayamba kwandandalitsa mpambo [5] wautari nakafika pa dambo pomwe adapangana. Ndipo Gwape anati, "Kamba tiye tiyambe kutamanga." Ndipo Gwape analiutsa liwiro atamangatamanga, naitana, "Ye Kamba!" Kamba nadawira patsogolo nati, "Ye! ndapita kale ine." Gwape uja anayamba kutamangansi naitananso, "Ye Kamba!" Kamba nati, "Ndapita kale ine." Ndipo Gwape adangolepera.

XVII

NSATU YA MITU IWIRI

I. Panali nsatu ya mitu iwiri inali yeitari, ndipo inaimba nyimbo yache niti, "Ngingiringi kuenda ati ngingiringi kuenda ati ngingiringi." Mbuyo mwache mulikubvomereza chokachokacho[1]. Ndipo inapangira chamba chache nitsokomola[2] wopo! wopo! wopo! inamvanso mbuyo wopo! wopo! wopo! Ndipo anafunsa, "Amene alikundiyeseza[3] nd'ani"[4]? Natuma amnyamata ache kuti, "Kamwiyang'aneni[5], mukamfeza mukampe"[6]. Iwo ananka alikulondalonda[7] bambo wao'yu, naturukira pomwe idalekeza nati, "Kodi timpe, tikampa safa'i, tiyeni tingomleka. Ndipo ananka kukamuza kuti, "Nanga tupi n'limodzimodzi tipa bwanje?" Koma nsatu inakwia kuti, "Mwamlekeranji ine ndimafuna kuti mumpe." Ndipo anapalizanso chamba, natsokomola wopo! nati, "Pitani musakamsianso'i, lero mukampe." Ndipo amnyamata anafika pomwe panali mutu wa chiwiri, nadula pa kosi, ndipo akabwera, alikuola; akati atsokomole[8], osatsiriza'i, amangoti, "Wopo! 'opo! 'po!" ndi mau ang'ono, naololà nafa.

XVIII

KACHIRAMBE

I. Ana a akazi[1] adati, "Tiyeni tinke, tikachere[2] ndiwo." Pamene analikuchera mwana wina anao-

na dzira la fisi, natola, naika m'nsengwa mwache, nauza anzache kuti, "Ana inu[3] ine ndafitsa[4] ndirikunka." Ndipo anzache anati, "Kodi mwachera ndi liti ndi liti[5] m'mene mulinkunka?" Ndipo iye anati, "Ine ndadzaza kale yanga nsengwa"[6]. Anzache anati, "Pita." Pamene wachoka anaona fisi wafika nafunsa kuti, "Ana inu watenga dzira langa apa nda'ni"[7]? Ndipo iwo analandula[8] kuti, "Kaya, koma amene wachoka nyalo[9] ndiye[10] watenga." Ndipo fisi anamuka, alikulonda[11], nafika nati, "Watenga dzira langa nda'ni"[12]? Ndipo mai wache anati, "Koma mwana'yo ndiye wabwera ndi dzira, liri pa moto." Fisi anati, "Nanga ine ndita-ni?" Ndipo muntu wa mai uja anati, "Linda ndi-kabala[13] mwana, ameneyu ndiye mudzadia iwe." Fisi nati, "Inde."

II. Tsiku lina muntu wa mai uja, pamene anachoka kunka ku madzi[14], fisi anafunsa kuti, "Kodi wabala mwana uja?" Mkazi anati, "Iai koma sindinabale." Masiku onse fisi alikunena chokachokacho[15], ndipo tsiku lina fisi anati, "Ukapanda kubala msanga, ndidia iwe amene"[16]. Ndipo mkazi'yo anaona tuza pa nsongolo pache, liri nenge! nenge! Ndipo linapulika tuza'lo, panaturuka mwana, ali ndi uta wache, ndi podo lache la mibvi, ndi chiguru chache cha mankwala, ni mpeni wache, ndi agaru ache, ndipo anati, "Ndaturuka ine Kachirambe mwana wobadwa pa nsongolo." Ndipo mai wa Kachirambe uja pamene ananka ku mudzi, anafunsanso fisi kuti, "Kodi mwana uja mwabala?" Ndipo mkazi uja anati, "Inde ndabala, ndipo mwana'yo ngochenjera kwambiri, simuta'i kumgwira, koma ine yemwe ndikunyengere, iwe ndikumanga, m'mtolo mwa udzu, ndipo ndikamuza Kachirambe kuti, 'Kasenze mtolo wa udzu, uli pa njira'po.'" Ndipo fisi uja anammanga m'mtolo mwa udzu, muntu wa mai uja namuka ku mudzi, nakauza mwana wache kuti,

"Kasenze mtolo wa udzu, uli pa njira'po." Ndipo Kachirambe anamuka, naima patari, nati, "Mtolo iwe tadzuka ndikusenze bwino." Ndipo mtolo uja unadzuka woka. Kachirambe anati, "Mtolo wanji wodzuka woka? Ine sindinaone woti choincho, ndipo toto [17] ine kunyamula." Namuka ku m'dzi.

III. Fisi uja anabwera namuza mkazi'yo kuti, "Mwana wako uja inde, 'ngochenjeradi." Ndipo adamuza fisi kuti, "Lero ndimnyengera pa diwa lo makoswe." Namuza Kachirambe kuti, "Kachere diwa, taona makoswe alikuta nsengwa." Ndipo Kachirambe uja anatenga mwala wa tantwe, natenga panda ndi mtanda wache, ndi luzi, natenga kapirimwana, namangirira, atenga nyambo, natira m'diwa'mo, nata. Madzulo fisi anabwera pa diwa, nagwetsa diwa'lo. Mai wache wa Kachirambe anaitana kuti, "Kachirambe diwa lagwa." Ndipo Kachirambe anati, "Diwa iwe igwanso [18] ndidziwe kuti lagwira koswe." Ndipo fisi ali pa diwa, nyamu! pi [19]! Kachirambe anati "Diwa lanji logwa kawiri sindinalione lotere."

IV. Ndipo mai uja wa Kachirambe anamuzanso fisi kuti, "Lero ukadikire [20] pa mtengo wa nandolo, ndikamuza mwana wanga kuti akachere nandolo." Ndipo Kachirambe anamuka, natenga nsengwa yache, nasanduka bemberezi, fisi uja angoyang'anira kuti, "Nyalo [21] abwera." Wangoona kuli zi! ndipo Kachirambe anafitsa [22], nabwera kumudzi, mai wache anazizwanso kuti, "Watenga kuti nandolo kwina [23] uli mtengo umodzi woka wa nandolo?" Ndipo mai uja anati, "Lero ndikamnyenga kuti katenge nkuni, ndipo ukampanikiza pompo." Namuza Kachirambe kuti, "Kateme nkuni m'tengo." Koma mwana uja analota kuti, koma lero ndikafa, natenga uta wache ndi podo lache, ndi chigulu chache cha mankwala, ndi chimpeni chache, nanka nakwera m'mtengo, nayamba kudula; ndipo anaona fisi wa-

fika, ali [24], " Wafa lero supulumukai ndikudia, tsika msanga m'mwamba'mo." Kachirambe ndipo anadula mtengo nati, " Ndirikutsika, yasama." Ndipo fisi uja anayasama, ali, " Tsika." Kachirambe anadawira kuti, " E, ndirikutsika." Naponya mtengo, ndipo unalowa ku kamwa kwa fisi, nafa; agaru ache poti akalume, nafanso. Kachirambe natsika, natenga mankwala ache, nawaza agaru ache, nadzuka. Pamene wanka ku mudzi anaponya mubvi kuti, " Ndidakutani [25], poti udzinditumizira zirombo kuti zindidie?" Ndipo mai wache adapepeza [26] kuti, " Pepa, mwana wanga mlandu uta m'pa kamwa " [27].

XIX

KALULU NDI MKANGO

I. Kalulu adakumba mbuna yache kuti adzipa [1] nyama, nafolerafolera bwino bwino, ndipo anatenga nkwangwa yache napachika pamwamba, nayamba kulira kuti, " Mai mai." Ndipo anafika Mbawala, nati, " Kodi ulikuliranji?" Kalulu anati, " Panabwera Mpoyo ndipo wandipachikira [2] nkwangwa yanga mwamba." Mbawala anati, " Pomwepa, ndipo mulepera kutsitsa weka, koma ndikutsitsire ine." Poti atsitse, anagwa m'mbuna'mo, Kalulu nalumpa, nakatenga nkwangwa natema Mbawala, napachikanso nkwangwa pompo, nafoleranso mbuna, nayamba kuliranso. Nabwera Njati, " Uliranji mwana'we?" Kalulu anati, " Panabwera Mpalampala ndiye wandipachikira nkwangwa yanga m'mwamba." Njati inati, " Pompa, ima ndikutsitsire ine." Poti atsitse, nalowanso m'mbuna'yo, Kalulu

nalumpanso, nakatenga nkwangwa, nampa nayo Njati. Nubwera Mkango, " Ulikuliranji kalulu?" Ndipo iye anati, " Kunabwera Njobvu ndipo wandipachikira nkwangwa yanga." Mkango unati, " Taima ndikutsitsire ine." Poti atsitse, nugwa m'mbuna'mo, koma Kalulu nayenso nagwa momo, ndipo Mkango unamgwira nati, " Bwanje unandinyenga kuti ndigwe, ine tsopano ndikupa." Ndipo Kalulu anati, " Pepani wawa [3], koma ndine muntu wanu kuti muli ndi ana [4], ine ndidzikanilerera [5] ana anu." Mkango udadawira [6] kuti, " Ana anga alipo awiri, ameneyu ndiwo udzikalera iwe."

II. Ndipo adanka ku mudzi kwa Mkango namuza kuti, " Ana amene udzilera iwe, nao." Mkango udanka kutengo kukasaka [7] nyama, ndipo pobwera akamwiitana Kalulu kuti atengere ana nyama kuti, " Iwe Kalulu ukadia mafupa, ana'o udzikapatsa minofu, chifukwa mano ao sanakwime." Koma Kalulu anamuka ali, " Ana inu [8], nali fupa [9], inu mudzadia kuti mukwimitse mano, ine ndidzadia minofu." M'mawa mwache [10] Kalulu anauza ana kuti, " Tiyeni ku madzi tikasewere." Pamene anafika ku madzi Kalulu anati, " Tiyeni tigwirane tiwone yemwe ali ni nyonga." Mwana wa mkango nagwetsa Kalulu ndipo Kalulu anati, " Musandipa mukapa ine, anilondera nd'ani ku mudzi?" Ndipo anamleka, Kalulu uja nasandulika, nampotola, ndiye kutenga mwana wina'yo kunka naye [11] kunyumba. Ndipo bambo anamwiitana Kalulu kuti, " Nayo nyama [12] ukapatsa ana'o, nanenso lero ndibwera pompo ndidzaone ana anga." Ndipo Kalulu ananyamula mwana, namonetsa kuti, " Ona nayo " [13]. Anyamulanso ali, " Wina nayo." Koma ananyamula mmodzi yeka yeka'yo [14]. Tsiku lina Kalulu anati, " Tiyeni tikasambenso." Nayambanso kusewera, ndipo mwana wa Mkango amgwetsa Kalulu kuti, " Wayesa muja [15] unandipera mbale wanga." Kalulu

anati, " Ukapa ine, unka ndi ani ku mudzi?" Ndipo anamleka, Kalulu anapendulika, nampanso, ndipo anati, " Nanga momwe [16] ndapa onse ndikanyengezeranji ku mudzi koma ndingokwera m'kankande, ndikokandidwekandiwe." Ndipo anakwera, nadziponya yeka [17], tsaka! tsaka! tsaka! nakandidwa tupi lache, natamanga kukanena [18] kwa mkango kuti, " Bambo sindinaone zabwino lero, ana aja apa [19] lero, taonani ine ndachita kupulumukira [20] pang'onong'ono, anati ape ndine yemwe." Mkango unati, " Wāzindikira?" Kalulu anati, " Ndadziwa ena ndinka ndikwazindikira."

III. Ndipo iye adanka, nafika ku mudzi wa Anyani afeza eni ache alikuponya nsikwa alikuti, " Manja'o " [21]. Ndipo Kalulu anati, " Atsamwali anga tiponye tonse, pamene ndiponya ine ndikati, adadia mwana wa mkango nd'ani, inu mudziti [22], ndine, ndine, nzabwino zimenezi tidzitero nafe masiku onse." Kalulu pochoka anati, " Anna inu ndibwera mawa tidzaponyanso. Ndipo Kalulu anachoka kunka kwa Mkango kuti, " Aja adapa ana ndapanikiza lero." Mkango unati, " Tiye tinke tonse ndikaone." Ndipo Kalulu anati, " Koma ndinimange m'mtolo." Naumanga natenga dzipatso nasomekasomeka m'mtolo kuti anyani adzikakondwera kuti, " Bwenzi latu labwera ndi chakudia lero." Ndipo adafika pa m'dzi pa Anyani nati Kalulu, " Ndabwera turutsani nsikwa tiponye." Ndipo adayamba kuponya, ndi [23], " Adadia mwana wa Mkango nd'ani, ndi pano ndi pano [24] sanabwere?" Anyani anati, " Ndine, ndine." Kalulunso anati " Mtolo kadzimvere " [25]. Ndipo mtolo unayamba kumasuka, mkango nubvumbvuluka nugwiragwira anyani onse.

XX

KALULU NDI NJOBVU

I. KUNJA kudauma gwa, wopanda ndi madzi omwe, nyama zonse zidangosauka, ndipo Njobvu inati, " Inu tidzafa tiyeni tikape chitsime." Ndipo nyama zonse zidasonkana, kunka ku dambo [1], ndipo Njobvu inati, " Ndiyambe ine kuponda." Niti [2], " Ndiponde apa pali madzi ndiponde apa pali madzi." Nangoona fumbi liri pwi! ti! ti! Ndipo Chipembere chinati " Taimani ndikayesa ine kuponda." Nati, " Ndiponde apa pali madzi." Nangoleperanso. Nyama zonse zinalepera, ndipo anaturuka Kalulu nati, " Taimani ndiponde ine." Ndipo akulu akamtsutsa kuti, " Kodi iwe ndiwe ukaponde, kapazi kakang'onong'ono, taona pazi langa lifana ngati [3] tako la mtondo." Ndipo Kalulu anati, " Ndikangoyesera, zikakandichimwa, zikandichimwire konko " [4]. Nayamba kuponda, " Ndiponde apa pali madzi, ndiponde apa pali madzi." Ndipo anaona chinyezi chiri eh [5]! Ndipo inabwera njobvu, iri, " Tachoka ndiponde ine." Napondaponda, nangoonanso fumbi liri tolo! tolo! ndiponso anati, " Tabwera Kalulu udzayesanso." Ndipo adangoona chidziwe chiri nde nde nde, nyama zonse zinamwa. Nilengeza [6] Njobvu niti, " Pasaoneka Kalulu wina amene adzamwa madzi pano, koma Kalulu yemwe'yo wabola madzi, ndiye adzimwa " [7]. Ndipo Akalulu anati, " Ha! ife sitinaone zotere, madzi wobola mbale watu yemwe, ndiwo adziti Akalulu asadzamwa " [8]. Ndipo Njobvu inati, " Ndikala mlonda ndidziona amene adzamwa madzi pano." Ndipo Akalulu adapangana kuti, " Ana inu tiyeni titengeni nkwangwa tidzinka ndi kufulira [9] njuchi."

II. Ndipo Kalulu anabwera nati, "Icho, icho, icho" [10]. Njobvu inati, "Kodi iwe ndiwe ani" [11]? Kalulu anati, "Ndine ndiri ni tidzitsopetsope, totsopitsa akulu atāmanga" [12]. Ndipo Njobvu inati, "Tiwone n'talawa" [13]. Kalulu anapereka chigulu, "Nachi" [14]. Njobvu nipisa chitamba chache nitseteka niti, "Inde nzabwino, mange." Ndipo Kalulu anatenga dzingwe dzache naimanga nanka nakamwa madzi, nachoka [15]. Njobvu inati, "Kalulu ulikuchoka osandipatsa" [16]. Kalulu nangochoka. Ndipo Njobvu inalira, "Ana inu dzandimasuleni [17]". Anzache nabwera nati, "Kodi wakumanga iwe ndani" [18]? Ndipo Njobvu inati, "Kalulu anabwera ndi dzitsopetsope anati n'dzotsopitsa akulu atāmanga [19], ndipo ine ndinati, 'Mange,' nandimanga ndipo anamwaimwa [20] madzi natawa." Ndipo Kamba anati, "Lero ndidikire ine." Njobvu inati, "Mwana'we Kamba iwe wokwekwerera kwekwerera pansi ndiwe ugwire Kalulu." Ndipo Kamba anati, "Iai tandimatani pula, ndimgwira pompano." Ndipo anzache anammatamata pula, namwiika pa madzi, nangokala msana wache tundulu, poyera. Ndipo Kalulu anabwera nati, "Wodi! wodi" [21]! Waona kuli nje. Ndipo anafika pa madzi'po, ayang'aneyang'ane [22] wafeza palibe antu. Ndipo anati, "Koma ndimwere pali mwala'po," nafika nalumpa pa msana pa Kamba, namwaimwa. Poti, "Tsopano ndiyambe kuchoka" [23]; anaona njutu! njutu! Ndipo Kamba anayamba kulira kuti, "Ndamgwira ndamgwira bwerani." Ndipo nyama zònse zinabwera. Kamba nabvulira pamodzi ni Kalulu, wina nagwira Kamba wina nagwira Kalulu, namtotola, ndipo Kalulu anati; "Inu mukati mupe ine, mukandigwira m'tu, moyo wanga mwini, mukandigwira mwendo, moyo wanga mwini, mukandigwira mchira, imfa yanga."

III. Ndipo anamgwira mchira, poti ammenyetse pansi mchira unapululuka. Kalulu natawa nanka

kwao, nakauza anzache kuti, "Kwadza chipulula mchira, taonani wanga'o ndapulula kale, ati akaona muntu osapulula mchira ameneyu amgwira, ati"[24]. Ndipo pa m'dzi pao Akalulu anapululana michira, onse, Ndipo Njobvu inabwera irikulonda[25] mapazi pa dimba, nati Ndanigwira lero, nd'ani uja anadzamwa[26] madzi." Ndipo Kalulu anati, "Kaya ife ndife Akalulu nsanga[27] sindife Akalulu iwo iwo[28], taonani ife tonse ndife wopanda mchira, mukaona wa mchira si pa m'dzi patu pano'i." Ndipo Njobvu idangolepera, nanka kwao. Inatera pompo[29].

XXI

TAMBALA NDI NAMZEZE

1. TAMBALA ndi Namzeze anapalana chibwenzi. Ndipo Tambala anaitana Namzeze, kuti, "Ubwere kwatu tidzacheza." Tambala anauza mkazi wache kuti, "Akafika[1] kuno Namzeze, udzamuza kuti, "Abwenzi lanu[2] si'wo[3], ali apo, ati wadula mutu, wazizwa"[4]. Ndipo Namzeze anabwera, nati, "Abwenzi latu ali kuti?" (Tambala anatenga mutu wache naika m'piko lache kuti bwenzi lache adzidzati[5] wadula ni mpéni.) Ndipo mkazi wa Tambala anati, "Si 'wo, ali apo, ati wadula mutu, wazizwa." Ndipo Namzeze anangokalakala, nadinadina[6], nanka kwao, osawonana naye. Nayenso Namzeze ananka ku nyumba kwache, nauza mkazache kuti, "Lero ndikaitana bwenzi langa Tambala, akabwera kuno, udzamuza kuti, "Abwenzi lanu wadula mutu wazizwa." Ndipo Tambala anafika nafunsa mkazache wa Namzeze kuti, "Abwenzi latu anka ku-

ti? Mkazi uja anati, " Abwenzi lanu si 'wo, ali apo, ati wadula mutu wazizwa." Ndipo Tambala ayang'aneyang'ane [7] osaona [8] kudzuka konse, chifukwa Namzeze adatenga mpeni nadula mutu wache. Ndipo Tambala adachoka kunka kwao [9], nakagona masiku atatu, nabwera ku nyumba kwa Namzeze nati, " Abwenzi latu ali bwanji tsopano tisalikwaona kubwera kwatu kudzacheza " [10]. Ndipo mkazi wa Namzeze anati, " Kaya nafenso chikalire chomwe chija " [11]. Konko ndiko kunalikupita Namzeze.

11. Koma mbale wa Namzeze anakapalananso chibwenzi ndi Tambala kuti, " Ndiwone nane " [12]. Ndipo Namzeze anati, " Tambala takondana nditu ndi iwe ndi ine sitilekana'i." Ndipo Namzeze anauza mkazache kuti, " Lero upike maungu, ndikaitana bwenzi langa Tambala, akabwera akadzafunsa kuti, " Bwenzi langa lanka kuti," " Iwe udzati, Abwenzi lanu ali umo." Ndipo Tambala anabwera nafunsa, kuti, " Abwenzi langa ali kuti?" Ndipo mkazi anati " Abwenzi lanu ali umo." Tambala ayang'ane wapeza mpika ulikubwadamuka ndi moto. Ndipo Tambala anazizwa kuti, " Abwenzi latu'wa aturuke'mo m'mene'mo." Ndipo mkazi uja anabvundukula mpika, ndipo Namzeze anaturuka msanga, deru alowa m'kati mwa utsi, monga ngati alikuturuka m'mpika, nakala pansi, nati, " Ah tinali m'menemo tamva kulankula mkazi, tapakula maungu'wo tidia ndi alendo." Ndipo mkazi uja anapakula napatsa, nayamba kudia ndi abwenzi ache. Koma Tambala ananka kwao, nakauza mkazache, kuti, " Mawa upike maungu ndikaitana bwenzi langa, ndipo ine undiike m'mpika momo, akabwera Namzeze udzati, " Abambo a kwatu ali m'pika'mo." Ndipo mkazi anati, " Kodi simupsai?" Mwini wache anati, " Iai bwenzi langa anachita choincho, adampika mkazache, ndipo nanenso ndirikuti undipike, akabwera Namzeze ndipo udzandibvundukule

ndipo ine ndidzatsata ndi utsi.'' Ndipo mkazi uja anatenga maungu natemeratemera m'nkali, naika pa moto, natsira madzi, natenga nkuni, natyolera tyolera pa moto, naika mwanna wache m'mpika'mo, nabvundikira. Ndipo mpika wache unayamba kuwira, koma Tambala uja anayamba kupipapipa'momo, ndiye kufa m'menemo. Mkazi uja akangosonkesabe nkuni. Ndipo bwenzi lache Namzeze anabwera nati, '' Abwenzi latu ali kuti,'' Ndipo mkazi uja anati, '' Ali m'mpika'mo.'' Pamene anabvundukula mpika anaona ubwea uli nyankwiriri, ndipo mkazi uja anati, '' Kodi umeneyo ndi moyo?'' Ndipo anayamba kupakula, anaona mwanna sanadzuke, ali lobodo. Namzeze anati, '' Kodi abwenzi latu unapika?'' Ndipo mkazi wa Tambala anati, '' Anachita kundiuza [13] kuti, ' Pike.' Ndamfunsa kuti, ' Kodi simupsa'i,' ndipo eni ache'wa anati, ' Iai sindipsa, bwenzi langa anachita choincho, sindipsa'i ine.' '' Ndipo Namzeze anati, '' Wachita choipa.'' Koma pamene ananka kwao anakambira anzache kuti, '' Ndidakamnyenga Tambala, ndipo anampika mkazache, iye akangoti wachenjeretsa ife, nafenso tidamnyenga, wafa, ngati [14] mbale wanga wafa kale.''

XXII

KAMBA NDI NYANI

I. Kamba ndi Nyani adapalana ubwenzi, ndipo Nyani adauza Kamba, kuti '' Ubwere kwatu tidzamwa moa.'' Moa utapsya [1], Kamba anachoka kunka kwa Anyani [2], anafeza atakwera [3] pa mtengo

ndi moa wao. Kamba adamuza kuti, "Kwerani momuno [4] ife moa watu sitimwera pansi." Kamba akati akwere [5] atereereka ndiye kungolepera. Anyani anati "Nao moa [6] musia noka." Ndipo Kamba ananka kwao, nakapikitsa wache moa [7], nakaitana [8] Anyani, atenta lupsya lache, moa wache akazika pakati pa lupsya, ndiye kutsuka [9] tsuka chiko chache. Anyani pobwera, anapondaponda lupsya, ndipo Kamba anati, "Taonani chiko'chi n'cha eni ache, ati musamagwira ndi dote, ati tsogolani mukasambe [10] m'manja" [11]. Anyani aja anka akasamba, pobwera, adzapondanso [12] pa lupsya. Kamba nanena "Musia noka moa."

XXIII

KAMBA NDI KAMUNDI

I. Kamba adakwatira pa mudzi pena, ndipo Kamundi adakafunsira [1] pa mudzi pokapoka'po [2], chifukwa adachitira chikamwini [3] anaona anali osauka; akala anali ndi chuma [4], bwenzi adakalowola [5]. Ndipo mpongozi wao anāgawira [6] minda kuti, "Kamba adzilima [7], nalowa uko, Kamundi adzilima, nalowa uko." Ndipo akayamba kulima m'minda mwao, Kamba akangoti—

"Fulukutu fulukutu, ali ku mudzi adziti alima."

Kamundi akati—

"Go! ndatema, Kamundi mungondida."

Ndipo adaona kwa Kamundi kuli kupu! kwa Kamba tengo liri gu! Ndipo tsiku lina mpongozi wao anati, "Ndifuna kukaona ku minda komwe alikulima akamwini anga." Pamene anafika anaona kwa

Kamundi n'kolimidwa, naona kwa Kamba kulibe ndime, ndipo anati, " Ndidangosanka mwanna osata kulima, mwanna koma Kamundi, ndipo ayesera kulima." Ndipo Kamba anamuza kuti, " Ukateme mtengo uja uli pakati pa munda, ukakapanda kugwetsa udzachoka pompano." Ndipo Kamba uja anasinka kuti, " Kodi ine ndikatema bwanje mtengo'o, ngati [8] ndita kukwera m'mwamba koma ndipale bwenzi kapena ameneyu angakanditemere?"

II. Ndipo Kamba anaona Simba nati, Simba, ndiwe bwenzi langa [9], ukanditemere mtengo ku munda kwa mpongozi wanga." Ndipo Simba analawira m'mawa mwa mpepo, nafika pa mtengo'po, naduladula. Pamene kwachetsa [10] kunja, Kamba anatenga nkwangwa yache kuti, " Ndikadule mtengo wanga." Ndipo akamuka alikukwawa, nkwangwa yache naponya m'tsogolo nakwekwerera. Pamene anafika pa mtengo anaona kuti Simba waduladula, nasadzirasadzira, ndipo Simba anachoka natsala mwini wache Kamba, alikungodula pang'ono pang'ono. Pamene waona mpongozi wache, ndipo kukangazakangaza. Mpongozi uja adadabwa kuti, " Ah! Kamba wadula choinchi mtengo uja, tsopano akala mkamwini wanga sachokanso'i." Ndiponso naye Simba kwao kudagwa maliro. Ndipo Simba ananka kukaitana [11] Kamba kuti, " Kwatu alikuika mafumu [12] ena atsopano, ndipo iwe bwenzi langa, nawenso [13] ukandilombole lero, pamene ana ena adzafika, alikuchula maina ao, iwe udzakale chete, ukadzamva ine ndirikuti, ' Ndafika ine Simba kuti ndilondoloze antu, iwe udzadawira, ndipo ufumu udzakala wanga." Ndipo Kamba uja anangochoka ndi usikusiku, nakafula pa litinda [14], nalowa pompo. M'mawa pamene kwacha anasonkana antu onse bi, ndipo ananyamuka mwana mmodzi nati, " Ndafika ine uje, ndirikuti ndilondoloze antu ine." Ndipo pa manda paja adaona pali ndu. Ndipo pa-

nabweranso mwana wina, nati, "Ndabwera ine uje kuti ndilondoloze mudzi wako." Pa litinda pali zi. Ndipo anyamuka Simba nati, "Ndabwera ine Simba ndirikuti ndilondoloze antu ako." Ndipo antu onse anamva pa litinda paja kulankula, kuti, "Ea ndimafuna iwe mwana wanga Simba kuti undilondolozere antu anga bwino." Ndipo antu onse anakondwera nanyamula Simba kumwiika pa pusi, madzulo ache[15] Kamba anaturuka kunka kwao[16].

III. Ndipo kwa Simba anapika moa, nakaitana Kamba, ndipo Kamba anauza ana a pa mudzi kuti, Tiyeni wandiitana bwenzi langa tikamwe moa." Ndipo ana a pa mudzi akamtsutsa, kuti, "Umuona kuti bwenzi iwe Kamba?" Ndipo Kamba anati, "Tiyeni mukaliwona bwenzi langa lopambana inu." Ndipo Kamba ananka nao ana aja a pa mudzi, nafika pa mudzi wa Simba, Simba natengeratu mphasa, namwiyalira. Ndipo akaturutsa moa, namaikira Kamba kuti, "Nazo zakudia"[17]. Nayenso Kamba napitiriza ana a pa m'dzi, namwa imwa[18] moa'o, ndipo anatsalitsa[19] bwenzi lache. Pamene wafika ku m'dzi kwao, ana aja akasimba kuti, "Kamba'yo ndi mfumu, musamamtsutsa, ife lero takaona ndi maso atu, bwenzi lache la Kamba ndi mfumu yopambana."

XXIV

WOPUNDUKA MASO NDI WOCHOKA MSANA

I. Kale mfumu idamanga mudzi wache ndipo pa mudzi pache'po pakabwera mikango kudzagwira[1] antu. Ndipo mfumu inati, "Kodi tichita nao chiani mikango'i?" Ndipo antu ache anati, "Yanku-

lani nayo." Ndipo mfumu anaifunsa kuti, "Kodi bwanji mulikugwira antu masiku onse?" Mikango inati, "Tirikuti mutipatse ana ako a akazi awiri omwe mukondana nao; iwe ukatipatsa[2] ana ako'o, sitidzabweranso kudzagwira antu." Ndipo mfumu idatenga ana ache awiri, nakamangira msasa ku piri, komwe inaturukira mikango. Ndipo ku dziko lina kunachoka antu awiri, wina Wopunduka maso, wina Wochoka msana, analinkunka ku mudzi wa mfumu. Ndipo Wochoka msana adaona kamba pa njira, nauza mzache kuti, "Pano pali kamba." Wopunduka maso adati, "Tola." Wochoka msana adakana. Wopunduka maso adati, "Tolera ine." Namtolera naika m'tumba mwache. Aendaenda anka pena, akapeza padafera nungu. Wochoka msana adati, "Pano pali nungu." Mzache anati, "Tola munga umodzi." Nakana. Wopunduka maso nati, "Tolera ine"[3]. Namtolera, naika m'tumba, nanka pena nakapeza padafera njobvu ndi muntu yemwe adalasa njobvu nayenso wafanso, mfuti yache iri pomwepo. Wochoka msana adanenanso kuti, "Pano padafera njobvu ndi muntu ni mfuti yache iri pomwepo." Ndipo mzache anati, "Tola mfuti ndi nyanga umodzi." Iye nakana, Wopunduka maso nati "Tolere ine."

II. Pamene anaona kuti dzuwa linalikulowa Wochoka msana adakwera pa piri, waona patseri palikufuka utsi, ndipo anapita pomwepo napeza anamwali awiri ali m'msasa'mo, nati, "Kwatidera[4] tifuna kogona." Koma anamwali adakaniza kuti, "Musagona pano, ife nyumba anatimangira atate watu, kuti mikango ikabwera, idzafikire[5] kutidia." Iwo aja adakana kuti, "Tigona pompano." Adakalankula, wafeza mikango yafika inkulira ndipo unafunsa, kuti, "Nda'ni[6] alikulankula m'nyumba-'mo, tinidiera[7] pamodzi." Ndipo Wopunduka maso anati, "Simungate kutidia nafenso[8] tatsata malo."

Ndipo mkango unati " Ndiniponyera nsabwe yanga muopa." Ndipo antu onse anakomoka, atsala muntu yeka Wopunduka maso; ndipo mkango unaponya nsabwe yache, Wopunduka maso nafufuza, natola nsabwe'yo, ali[9], " Aka taona ndi kaponya pa moto." Akaponya kapulika, ndipo anati, " Nanenso ndikuponyera yanga nsabwe "[10]. Naturutsa kamba wache naponya. Mkango utola uyang'ana, uli, " Ha! inde ali ni nsabwe yeikulu." Nati, "Iai sindiopa'i tsopano ndikuponyera ubwea wanga." Anatotola ubwea umodzi, naponya uli, " Nao[11] ndakuponyera." Wopunduka maso anaambasaambasa nati, " Umeneo ndio ndiope ine, tayang'ana wanga." Natenga munga wa nungu, nauponyera mkango, mkango unautola uyang'ana, uli, " Inde." Nuti, " Iai mungatero sindikulekani." Nutenga dzino lache, nuponya, Wopunduka maso napapasa, natola, nati, " Limeneli ndilo ndiope ine, taima ndikuponyera langa."

III. Ndipo anauponyera nyanga[12] wa njobvu, mkango nulumpa, uli, " Ha! inde muntu'yo ali ndi dzino loopsya." Koma unati, " Tsopano ndi kuomberani mau anga." Ndipo unayamba kubangula. Wopunduka maso anati, " Wina'yo ngālire[13] ache mau ndiwamve." Ndipo anati, " Ndamva, tsopano bwerani pafupi mumve mau anga." Ndipo mikango inadza pafupi. Wopunduka maso anati, " Muli pati?" Iri, " Tiri pano." Ndipo adati, " Gumitizani mitu pamodzi." Natenga mfuti yache naloza pompo nati, " Tsopano imvani ndikulankula anga mau." Naomba mfuti yache napa zonse'zo. Ali " Mwamva mau anga?" Wafeza kuli zi; ndipo anadzutsa anzache omwe anakomoka nati, " Dzukani zirombo zija ndapa." Akamtsutsa kuti, " Ulikutinyenga." Wopunduka maso anati, " Antuni dzukani, munditsegulire ku komo ndikayang'ane ndeka." Namtsegulira nanka afufuza ali, " Ichi

n'champongo ichi n'chachikazi, turukani panja pano mudzione noka."

IV. M'mawa mwache ndipo anachoka, mwana wina wa mkazi anabereka muntu Wopunduka maso, wina nabereka Wochoka msana. Pamene adafika ku mudzi, bambo wao adaona, nati "Kodi, mwabweranso, muja[14] ndinati mukale komweko, tsopano ndipa inu nonse." Ana aja anati, "Anazipa zirombo zija." Bambo uja nati "Kodi nzo'ona?" Ndipo aja anati, "N'dukeduke"[15]. Bambo natumiza amnyamata kuti, "Pita mukayang'ane." Amnyamata anafika nazipeza, nadula michira, akauza mfumu kuti, "Michira nai[16], adapadi." Ndipo mfumu inapangana ndi antu ache kuti, "Nanga antu awa wapa zirombo tichita nao bwanje?" Ndipo anati "Mungwakwatitsa[17] akazi omwe'o." Ndipo Wopunduka maso adampatsa wache, Wochoka msana wache natenga mpande[18] zisanu ndi imodzi, ali, "Wina zache zitatu, winanso zitatu mukamange mudzi wanu uku." Ponka pa njira Wochoka msana anati, "Ife watipatsa mpande zisanu, ati, iwe zako n'ziwiri, ine zanga n'zitatu." Wopunduka maso anati, "Ha, ulikundidierera, si muja mfumu yanena watipatsa zisanu ndi imodzi ine zanga zitatu iwe zako zitatu, nanga undichenjera bwanji muja ndikati tola ichi udakana?" Ndipo Wochoka msana anaimirira[19] nammenya ku maso, ndipo Wopunduka maso anapeza m'maso mwache mwatseguka, natenga ndodo namenya mzache. Wochoka msana napeza msana wache waongoka. Pompo ndipo anagwirana chanza[20].

XXV

MWAMBI (NTANU)

I. TIYENI tikachite mwambi lero, ndipo antu onse asonkana, nyumba tho! Nayamba m'modzi kunena kuti, "Chakuti chakuti [1] n'chiani?" Ndipo anzache akalepera [2] iye ati, "Baireni" [3]. Ndipo ambaira kuti, "Kadie [4] za kwa uje." Ndipo iye ali nazo gwa! nyama twē! nadia idia [5], nati, "Chimenecho n'chakuti."

Kantu kopanda nkwaso n'chiani?
Mubvi.

Kantu kosamangika'i n'chiani?
Mpepo (kapena *madzi*, kapena *utsi*).

Kantu konunkiza, ungabisitse kako kakalondola [6], n'chiani?
Nchenche.

Kantu koota moto n'kumbuyo?
Tsanja.

Antu nonse nkondo inichimwa [7], kantu kamodzi koputaputa, kakaiponya [8], n'chiani?
Mtiko.

Muntu akaponya mubvi wache kumwamba, ndipo pobwera ubwera wopanda bango, n'chiani?
Inswa. (Chifukwa pouluka ziuluka ndi mapiko, zigwa zopanda mapiko.)

Kantu kosanyamulika'i?
Chitunzitunzi.

Mtengo womera pa mtengo unzache n'chiani?
Ulimbo [9],

Kweru tsiku, kweru tsiku n'chiani?
Munsi.

Nyumba yapsya, watsala mtanda woka?
Njira (Chifukwa tengo likapsya itsala njira yoka, iri tanta).

Ndamanga nyumba ndi mzati umodzi, n'chiani?
Boa.

Antu awiri asenza chintu chachikulu n'chiani?
Mitanda iwiri isenza nkokwe.

Diwa lagwa kawiri kawiri lero loka loka n'chiani?
Chikope.

Chintu cholakwa antu onse, asenza muntu mmodzi.
Madzi.

Kantu kofuma kutari, kutifeza ife pano.
Mvula.

Muntu alima minda yambiri lero lomwe osatopa'i n'chiani?
Wometa.

Kantu kolondola koka, sikaphonya'i [10], kungakale mdima, n'chiani?
Dzanja (Chifukwa siiwala pa kamwa).

Mpini [11] umodzi, nsompo kumi.
Ntochi.

Nyumba yopanda komo.
Dzira.

Kantu kosaoneka komwe kadagwera.
Tambo.

Kantu kokalemekeza, kolira kukagwira ndi manja awiri.
Ntedza.

Nkalamba imweta udzu n'kumimba ni folera n'kumsana, n'chiani?

Chipande.

Mtengo adula lero, m'mawa mwache uyamba kupuka.

Tsitsi.

Kungatarikitsa, lero lomwe ukafika, n'chiani?

Mtima.

Pita uku, nanenso, ndipite uko, tikomane.

Mkuzi.

Chinyama chofa m'malimwe, pfungo lache limve ka kuno [12], n'chiani?

Mvula.

Nyama zipezana pa madzi.

Antu.

Mfumu idatumiza muntu [13] kuti akatenge mbuzi, ndi chimanga, ndi kambuku, ndipo pofika pa nyanja, anapeza bwato bwabwang'ono. Ndipo anati, "Ndiyambe chiani? ndikayamba kambuku, mbuzi idzadia chimanga, ndikayamba chimanga, kambuku adia mbuzi, koma ndiyambe mbuzi." Natenga mbuzi, naolotsa, ndipo anasinkanso kuti, "Ine ndikatenga chimanga mbuzi ikadia ndikatenga kambuku mbuzi ikadiedwa." Nanga muntu uja adatani?

Poyamba analowetsa mbuzi, inka patsidia, nabwerera natenga kambuku, natenganso mbuzi nabwezera m'bwato, akasia patsidia pomwe, natenga chimanga, nabweranso, nakatenga mbuzi.

Madzi akatayika saola.

Kwagwa mtengo sikuzimira'i.

Kako n'komwe wadieratu, mukapanda kudia n'kamwini.

Dote, sin'kadakudia, ndikudiera ku uchi.
Liwiro la m'mchenga, mumayambira pamodzi.
Chaona mzako chapita mawa chiona iwe.
Mwalemera nyanga yanga, sumandidia'i [14].

XXVI

CHAMBA CHA KANONOMERA

MUNTU akadwala [1], akaombeza ula [2] ndipo wa ula ati, " Pali mzimu wa gogo [3] wache ulikufuna chamba [4], mukabvina chamba'cho mundionere [5] mwana alikukala tsonga." Apita ku mudzi natenga nsengwa ya dzintu, nanena nazo kwa mzimu kuti, " Nao maere [6] amene mulikupera [7] muntu tikapika moa tiwone [8] muntu alikukala tsonga." Ndipo amema [9] antu onse, tsiku losuza [10] ndipo antu asonkana, madzulo ache [11] nalowa m'nyumba, nayamba kuomba m'manja kudzutsa [12] mzimu, ndipo aona muntu wodwala'yo alikuntuntumira ndi kulira [13], ndipo antu ati, " Musadza ndi nkhondo, taniitana ndife, taonani pam'dzi pano padza ng'oma koma zichoke bwino, musazichititsa ntenya " [14]. Akata kuombera m'manja, chamba chituruka panja, nayamba kuimba ng'oma, alikubvina. Wakumbuka nyimbo, naimba, muntu amene agwidwa ndi nzimu, agwa, namchotsa kunja, nayamba kumbveka nsaru ndi zikopa za nyama, nalowanso, nayamba kubvina. Muntu akagwidwa ndi mzimu wa mwana, ayamba kummangitsa nsaru yache, kuti ilimbe, chifukwa muntu'yo alikufuna kuti abvule nsaru yache kuti adzibvina maliseche, chifukwa mwana wa kanda sakabvala'i. Mka-

zi akagwidwa ndi mzimu wa mpongo kuti, "Ndine uje." Ambveka myoni, ku manja kwache nagwira katemo, amanga nsaru yache m'chuuno, mabere oka ali kwapa, kwapa. Nyimbo zache za chamba cha Kanonomera, anziti—

Chipunga lume [15],
Chadza m'mamawa.

So so tingoyang'ana,
So so tingoyang'ana.

Ng'oma ikalira,
Imtenga choinjoli [16].

Kutari kutari tari,
Kutari kutari tari,
Kutari kwayera mtambo,
Kutari kuli uta wanga [17].

Kamang'ani Kamang'ani katola maere,
N'kanje katole,
Ndi maso ache [18].

Idamchola myendo,
Njala yoka yoka.

Ai, ai, inde, inde,
Chalakwa [19] inde inde,
Chalakwa chiwiri [20] inde.

Mwandida ine,
Mwan'dera ukalamba.